

MULUNGU ALINAYO NJIRA

YOPEREKEDWERATU



Usiku wabwino, abwenzi. Ndi mwayi waukulu kuti tiri muno usikuuno mu nyumba yoyankhuliramo ino, kuti tidzatumikire kwa ana a Mulungu, kwa odwala ndi osautsika, ndi kuti tidzatumikire kwa osapulumsidwa, mwa njira ya chipulumutso. Ndipo ndife achisoni kuti uwu uyenera kuti ukhale usiku wathu wotsiriza mu msonkhano wokopa wapadera uwu, mndandanda wa misonkhano iyi, koma ndithudi ife tikufuna kuti tikuthokozeni mmodzi ndi wina aliyense wa inu chifukwa cha chiyanjano chanu chodabwitsa, chifukwa cha zonse zomwe inu mwatichitira ife, kutipatsa ife chikhulupiriro chanu, ndi zanu... zonse zomwe inu mwazichita. Ife tikuyamikira izo kuchokera pansu pa mtima wathu. Muyaya wokha udzafotokoza momwe ife tikuyamikirira.

² Ndipo ife tikufuna kuti tikhale oyamikira kwa M'bale wathu Cauble, chifukwa cha kutithandizira kwake ife muno mu mzinda; ndi chifukwa cha chiyanjano chabwino chimene ife takhala nacho ndi iye ndi mpingo wake, ndi anthu ake. Ndipo ife tikukuthokozani nonse inu omwe mwabwera kuchokera ku malo osiyana, kuchokera ku Indiana ndi kozungulira, maiko ozungulira. Iyo siinalengezedwe nkomwe uko. Ine ndikuganiza inu munangozimvera izo pa makalata, mwinamwake, kuti iwo udzakhala kuno. Chifukwa, ife tikudziwa kuti ife sitikanakhala ndi malo okwanira mu tchalitchi icho. Ndipo ife tikanaganiza, ngati izo zingayipe kwambiri, ndiye mwina ife tikanakhoza kudzapeza usiku kapena uwiri mu nyumba yoyankhuliramo.

³ Tsopano, ndife oyamikira chifukwa cha anthu omwe anatilola ife kuti tikhoze kukhala nayo nyumba yoyankhuliramo iyi usikuuno, pakuti ife tikuyamikira izo, chifukwa cha iwo potsegula malo ano kwa misonkhano iyi usiku wa Lamlungu uwu, kwa ulemerero wa Ambuye wathu Yesu Khristu. Ife tikumuthokoza Iye.

⁴ Ndipo tsopano, basi pamene ine ndinali kubwera muno tsopano pompa, m'bale wanga ndi Billy, ndipo ena a iwo anali ataima kunja uko, anandiuza ine kuti zinalipo ndalama zokwanira, mokwanira kuti alipirire ngongole zonse. Iwo alipira rendi ya tchalitchi ndi nyuzipepala, ndi osamalira pa malo a mpingo, ndi nyimbo, ndi zolengeza zonse za pa nyuzipepala, kulengeza kwa pa wailesi. Chirichonse chalipiridwa, mpakana usikuuno. Ine ndikuganiza iwo anali nazo zokwanira, chotero

izo zinapanga chopereka-chachikondi cha usikuwu kukhala chaulere kwa ine.

⁵ Izo, ine nthawizonse ndakhala ndikuyesera kuti ndisunge, monga inu mukudziwira, mbiriyanga pa ndalama. Ife sitimachita izo. Ndipo ngati palibe zokwanira kuti zisamalire zinthu, ndiye ine ndimachotsa izo kuchokera ku chopereka changa chachikondi. Ndipo chopereka chachikondi, ine sindikanati ndizitenga konse icho, ngati ine ndikanati ndisakhale munthu wosauka ndipo ndimakhala moyo monga ena tonse ife timachitira. Ngati ine ndikanati ndizigwira ntchito, ndikumayendetsabe misonkhano iyi kudutsa mfukoli, ine sindikanati ndizitchula nkomwe za chopereka chachikondi kwa inemwini. Zoti tilipire zokha ndi zonse zomwe ife timazisowa. Ndipo izo sizinakhale mu Louisville mokha, izo zakhala ziri kuzungulira dziko lonse. Ndipo momwe ine nditi ndikhalire moyo, ndipo Mulungu akamandithandiza ine, izo zikhala ziri mwanjira imeneyo. Osati ndalama; ine sindikufuna ndalama. Ine ndikuyesera kuti ndiwatengere anthu poti amukhulupirire Ambuye Yesu Khristu, kwa chipulumutso chawo ndi kwa machiritso awo.

⁶ Ndipo zakhumi zanu, ndi zina zotero, zomwe inu munaikamo, sabata yatha iyi, zapita kwa cholinga icho. Ndipo Lamlungu usiku, iwo kawirikawiri, kapena usiku wotsiriza wa msonkhano, chirichonsecho, ndi sabata kapena masabata awiri, masiku teni kapena chirichonse, iwo anatenga chopereka-chachikondi kwa ine. Ndipo ngati pangakhale chirichonse umo chimene chingatsalire, icho chipita molunjika kumene ku utumiki wamaiko akunja. Mwina mlembi wanga ndi iwo omwe amasalira za ndalama, ndi zina zotero, alipo pano tsopano, ndi mkazi wanga ndi iwo, amene akudziwa kuti izo ndi zoono. Ndipo Mulungu Wamphamvuzonse, Yemwe ali Woweruza wathu, akudziwa kuti izo ndi zoono. Ndipo kotero ife tikukuthokozani inu pa chirichonse chimene inu mwachichita.

⁷ Tsopano, uno pokhala usiku wotsekera wa msonkhano, tsopano ife tikayamba mawa ku Shreveport, Louisiana, tikayambira uko mu Nyumba yoyankhuliramo ya Municipal kwa misonkhanoyo; msonkhano wotsatira ndi woti ukayambe apo.

⁸ Ndiyeno ife tikapita kuchokera uko ku Denver, Colorado, kumene Amuna Amalonda Achikhristu, aku Denver, akutithandizira ife kumeneko, mu—misonkhano yokopa. Ndipo ine ndikukhulupirira ndi ku Yamzinda kapena Nyumba yoyankhuliramo ya Mzinda uko; kulibe mipingo yomwe ikuthandizira iyo, Amuna Amalonda Achikhristu okha.

⁹ Ndiyeno kuchokera uko, ife tikapita ku—ku Edmonton, Alberta. Ndiyeno kuchokera uko, ku Grand Prairie, British Columbia; Dawson Creek; mpaka mu dziko la ma Eskimo.

¹⁰ Ndipo ife tikabwereranso uko ndiye kachiwiri, cha mu, tikayambira kumusi uko mu maiko kachiwiri, cha mu Juni, komwe kuti kukakhale uko mu Des Moines, Iowa. Ndipo ife tikapita ku mabwalo a misasa a Methodisti ku Nyanja ya Cedar, mu msonkhano waukulu uko; ndiyeno mpaka Kumpoto chakummawa kwa Pacific.

¹¹ Ndiyeno kuchokera uko, ku Durban, South Afrika. Nthawi ino, uko si kusankha kwanga, dongosolo langa. Ndizo PAKUTI ATERO AMBUYE. Ndi kudzapita ku Afrika; India; Palestina; Luxembourg; Frankfurt, Germany; ndi London; ndipo kenako ku Paris; ndiye nkubwerera kwathu.

¹² Ndiye kuchokera uko, ife tiyenera kudzafika cha mu Januwale kapena Febuluwale, kuti tidzapite ku New Zealand, Australia, ndi mpaka Kummawa.

¹³ Ndipo ine ndidzakhala ndikuyembekezera mapemphero kuti azibwera kuchokera ku Louisville, Kentucky, mwa kuthandizira msonkhano uwu umene ife tikupitako, mu ndondomekoyi.

¹⁴ Imodzi ya nthawi izi, ngati ine ndingadzapezeke kuti ndidzabwerere ngakhale chaka kuyambira lero, alipo ambiri omwe ali muno usikuuno, mwina, sadzakhala ali pano, ngati ine nditi ndisungidwe. Mwa omvetsera ochuluka chonchi, o, anthu chikwi kapena kupitirira, chirichonsecho, adzakhala ali—adzakhala ali ambiri a inu mutapita. Ndiye ine ndidzacomana nanu inu kachiwiri, amodzi a mmawa waulemerero uwu, pa chiwukitsiro, pamene oyera (owomboledwa) adzabwezeretsedwanso pa dziko lapansi kachiwiri, ku Zakachikwi zopambana. Ine ndikuyembekeza kudzakhala Muyaya wosatha ndi inu mu Ufumu wa Mulungu, umene ine ndikuwuyimira pano usikuuno.

¹⁵ Mulungu akudalitseni inu nonse. Ndipo ine sindikufuna kuti ndimusiye kunja aliyense. Madona aang'ono omwe amayimba nyimbo ndi, o, aliyense, Mulungu akudalitseni inu.

¹⁶ Tsopano zagwera ine, usikuuno, kuti ndiyankhule mphindi pang'ono pokha kachiwiri. Ndipo ine sindikudziwa nthawi yomwe ife tiyenera kutseka mu nyumba yoyankhuliramoyi. Koma kuti ndiyambe pa nthawi yake basi, pa hafu pasiti eyiti, mwina ndiyankhula theka la ora; ndiye nkuyamba mzere wathu wa pemphero, kuwapempherera odwala.

¹⁷ Ndipo tsopano inu anthu okonedwa Achikhristu muno, aku Louisville, Kentucky, ndi Jeffersonville, New Albany. Limodzi la masiku awa, ine ndikufuna kuti ndidzalengeze msonkhano mwafuko, ndi kudzakhala ndi chihema chakale, chachikulu chachikale titachiika kuno, chomwe mungadzakhalemo anthu masauzande angapo, ndi kudzakhalamo ndi chitsitsimutso cha kachitidwe-kachikale. Ndicho chimene ine ndikuganiza ife tikuchisowa mu Louisville, ndi chitsitsimutso cha kachitidwe

kachikale, chotumizidwa ndi Mulungu. Inu mupemphere. Ngati Ambuye atitsogolera mwanjira imeneyo, ine ndidzabwera.

¹⁸ Tsopano pali misonkhano iwiri kapena itatu yokopa ya machiritso yomwe ikuchitika mu mzindawu. Ndi chifukwa ife sitinachipange ichi nkhani ya fuko lonse. Ife tinangobwera ku mpingo wa M'bale Cauble, mwaona. Ndipo ife sitinabwere kuno kuti tidzakhale opikisana ndi abale ena awa. Ife sitimakhulupirira mu kukhala opikisana mu chipembedzo cha Yesu Khristu. Ife ndi abale, palimodzi, tikugwira ntchito limodzi kwa onse omwe ife tingakhoze, kwa ubwino wa Ufumu wa Mulungu, ndi mpingo uliwonse, wina aliyense.

¹⁹ Ife tikhoza kumasiyana pang'ono pokha mu malingaliro, atumiki, koma osati kwa anthu. Ife tikukhulupirirabe Mwazi wa Yesu Khristu umatitsuka ife ku kusalungama konse. Ife timakhala ana aamuna ndi aakazi a Mulungu pa kuvomereza machimo athu ndi kuwalandira Magazi awa, ziribe kanthu kuti ndiwe wa mpingo uti. Ndipo ife timakhulupirira izo ndi mtima wathu wonse. Misonkhano yanga nthawizonse ndi ya uvangeli wokomera onse, kapena ya zipembedzo zonse, kotero ife tikudalira kuti Mulungu akudalitsani inu nonse.

²⁰ Tsopano, pa kuyima, makamaka, mu mzinda kapena malo, ife sitiri pano kuti tidzaimire machiritso Auzimu. Ife sitikuwonetsera nkomwe machiritso Auzimu. Ife tikuwonetsera Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu. Ndipo pamene inu mukuwonetsera Yesu Khristu, inu mumawonetsera machiritso Auzimu. Chifukwa, ndi zotsatira za imfa Yake, imene imatipatsa ife chipulumutso, ndi machiritso a matupi athu.

²¹ Ndipo mulibe a—ayi mphamvu mwa munthu aliyense, yomwe ingakhoze kumuchiza munthu wina. Machiritso anagulidwa kale pa Kalvare. Ndipo chinthu chokha chimene ife tingakhoze kuchita ndi kumulozera munthu kumene nthawimodzi iyo, Nsembe yokwanira zonse inapangidwa ndi Yesu Khristu Mwana wa Mulungu. Mmenemo, ife timangoyang'ana ndi kukhala moyo. Mulungu anakonza njira, ndipo ife timailandira iyo.

²² Mtumiki sangakhoze kumupulutsa wina aliyense; iye angakhoze kokha kulalikirira Uthenga, ngati iye ali wodzozedwa ndi Mzimu Woyera, ndi kuwalozera anthu ku malo kumene iwo anapulumutsidwako. Iwo anapulumutsidwa, zaka naintini handiredi zapitazo, pa Kalvare. Inu muyenera kumulandira iye ngati Mpulumutsi wanuwano tsopano, kuti mukhale nazo zopindula, kapena zogawiridwa, kuchokera pa imfa Yake, ndi kusangalala nazo zotsatira za zomwe Iye anazifera.

²³ Tsopano, ndipo machiritso Auzimu ali chinthu chomwecho. “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, anatunduzidwa chifukwa cha kusaweruzika kwathu, chilango cha mtendere wathu pa Iye, ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa,”

zonse mu tsiku lomwelo, ndi Munthu yemweyo. Zosalekanitsika, zimayendera limodzi, china kwa chimzake; Magazi obwera kuchokera ku nsana Wake, ndi awo omwe obwera kuchokera mmabala Ake, amasakanikirana limodzi ndi kumayenderera mpaka mmapazi Ake. Onani, ndi zimenezo. Chipulumutso, machiritso, mtendere, kukhutitsidwa, chimwemwe, chirichonse chimene ife tikuchisowa mu ulendo wa pansi pano, chinakomanidwa mu Kalvare. Ndipo Mulungu atumikira kwa aliynse yemwe ati avomereze izo pa maziko amenewo ndi kuzikhulupirira izo ndi mtima wawo wonse.

²⁴ Tsopano, “Mulungu anaika mu Mpingo, ena aphunzitsi, atumwi, aneneri, mphatso za machiritso,” ndi, o, mphatso za mitundu yosiyana. Iye anaziyika izo mu Mpingo “kwa kuupangitsa ungwiro Mpingo,” kuwutengera Mpingo palimodzi.

²⁵ Ndipo tsopano masiku adutsa kuyambira pa gulu loyamba kwa atumwi. Iwo anali nazo mphatso naini zonse zikugwira ntchito mu mpingo.

Gulu lachiwiri, iwo anayamba kuzilala.

Gulu lachitatu, zinali pafupi zonse zitapita.

Ndiye zinapita mu zaka ffitini handiredi za mibadwo ya mdima.

Ndiye panadza kukonzanso.

²⁶ Kutachitika kukonzanso, panadza kuyeretsedwa; pambuyo pa kulungamitsidwa kunadza Joni Wesile, akulalikira kuyeretsedwa. Mmenemo munadza Calvin, Knox, ndi onse awo omwe anadza mmusimo kupita mu Pentekoste, Nazerini, m’badwo umenewo.

²⁷ Ndipo tsopano ife tikusunthirabe kukalowa mu m’badwo wina waukulu, ukudzera Mkwatulo wa Mpingo. Ndipo mu uwu, ife tikukhala mu nthawi ya kubwezeretsa kwa mphatso. Izo zinawapunthwitsa ochuluka a mipingo yawo yabwino yaikulu; izo zinawatumiza Achinazerini cha mmbuyo; izo zinapanga otentheka mwa ochuluka Achipentekoste. Koma, mofanana basi, Mulungu akusunthirabe patsogolo, akubweretsamo Chikhulupiriro Chokwatulitsa kwa Mpingo Wake. Ndiko kulondola. Chotero, usikuuno, ine ndikuimira Chikhulupiriro chimenecho, “Chikhulupiriro chimene chinaperekedwapo kamodzi kwa oyeramtima,” mwa njira ya mphatso Yauzimu.

²⁸ Chimene, mwa kulingalira kwanga, “Mphatso ndi maitanidwe . . .” Osati lingaliro langa; koma Baibulo limanena, kuti, “Mphatso ndi maitanidwe ndi zopanda kulapa.” Palibe kanthu komwe inu mungakhoze kuchita nazo. Iwe sungakhoze kudzipanga wekha kukhala ndi maso a buluu pamene iwe uli ndi abulauni. Iwe uli basi chimene iwe uli, mwa chisomo cha Mulungu.

²⁹ Iwe sungakhoze ngakhale kubwera kwa Mulungu popanda Mulungu kukuitana iwe poyamba. Iwe sungakhoze kumufunafuna Mulungu popanda Mulungu kukufunafuna iwe poyamba ndi kukuitana iwe. “Palibe munthu angakhoze kudza kwa Ine, kupatula Atate Anga atamukoka iye.” Chotero, Mulungu akufunafuna. “Mulungu waika mu Mpingo. . .”

³⁰ Ndiyeno kuchokera pa mwana wamng’ono, wobadwira kuno mu dziko ili la Kentucky, masomphenya amangobwera kwa ine mofanana basi monga—monga kudya kapena china chirichonse. Izo zimangokhala monga momwe Mulungu angafunire, Iye amapereka izo. Ine ndimangochita momwe Iye amanduzira ine kuti ndichite.

³¹ Ndithudi, ine ndiri nawo onditsutsa ambiri. Ine ndiri nawo anthu ambiri omwe samakhulupirira izo. Ziribe kanthu zomwe zingati zichitike, iwo samazikhulupirira izo, mulimonse. Ine ndimayembekeza kukhala nazo izo. Ndipo ngati ine ndikanati ndisakhale nazo izo, ine ndikanati ndipite pansi pa guwa kwinakwake ndi kukati, “Wokonedwa Ambuye, chalakwika ndi chiani ndi ine?”

³² “Pakuti onse omwe amakhala mwaumulungu mwa Khristu Yesu adzavutika ndi kusautsidwa.” Kulondola. Ife timayenera kumakhala nazo izo. Ndiko kulondola.

³³ Chotero, Yesu anali nazo izo. Ndipo Iye anati, ngati. . . Pamene Iye ankakhoza kuima mwa omvetsera Ake, ndi kumadziwa chomwe (anthu) anali atalakwitsa, ndi momwe iwo anali atachiritsidwa kapena ayi. Ndipo iwo ankamukhudza Iye, ndi—ndi chikhulupiriro chawo. Pamene Iye anatembenuka ndipo anati, “Ndani wandikhudza Ine?” Iye anati, “Chikhulupiriro chako chakupulumutsa iwe. Tsopano kuwukha kwa magazi kwako kwatha. Chikhulupiriro chako chakupangitsa iwe kuchira.”

³⁴ Mkazi anadza kwa Iye nthawiyina. Kapena, Iye anaima pamene iye anali; pa dziwe, kapena malo omwela, chitsime, chitsime cha Yakobo. Ndipo mkazi anadza, ndipo Iye anayamba kukambirana naye kwa mphindi zochepa mpaka Iye anapeza vuto lake. Anati, “Pita ukamutenge mwamuna wako.”

Iye anati, “Ine ndiribe aliyense.”

Anati, “Uko nkulondola. Iwe uli nawo asanu.”

³⁵ Iye, pamene Iye anali kuno, Iye ankadziwa kumene kunali nsomba, imene inali ndi ndalama mkamwa mwake. Iye ankadziwa kumene abulu awiri anali ataima, atamangidwa, kumene njira ziwiri zimakomana pamodzi. Ndipo Iye ankadziwa kumene mwamuna akanakhala atanyamula mtsuko. Zinthu zambiri zomwe Iye ankazidziwa. Iye anamudziwa Filipino pamene iye anadza kwa Iye, kuti iye anali akupemphera asanabwere, pansi pa mtengo; ankadziwa kuti iye anali munthu wabwino, wachilungamo.

³⁶ Koma Iye anati, mu Mawu Ake Omwe, “Ine sindingakhoze kuchita kanthu mwa Inendekha, mpaka Atate atandisonyeza Ine choti ndichite.” Onse amene akukhulupirira Lemba limenelo, nenani “ameni.” [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndi zomwe ali, Yohane Woyera 5:19.

³⁷ Iye anadutsa pa unyinji waukulu, anthu masauzande awiri kapena atatu ali pamenepo; olumala, opindika, opunduka, osayenda, akhungu, opuwala; wodzaza nacho chikondi ndi chifundo, anayenda namudutsa aliyense wa iwo. Anamuchiritsa munthu wa matenda ena aang’ono, ngati. O, ine sindikudziwa; iye mwina anangokhala wosachedwa kuzidzidwa moipa, pa zonse zomwe ine ndikuzidziwa. Izo, iye anali nazo izo zaka sate-eyiti. Izo sizikanati zimuvulaze iye kapena kumupha iye; izo zinali zitamkanirira. Ndipo Iye anamupangitsa munthu ameneyo kuchira, ndipo anachokapo ndi kuwusiya unyinji uwo uli apo. Ndiyeno pamene Iye anafunsidwa, Iye anati, “Ine sindingakhoze kuchita kanthu mwa Inendekha, koma chimene ine ndiwawona Atate akuchichita.”

³⁸ Tsopano nthawizina anthu ankafuna kuti Iye azichita chisudzo nazo izo, pamene iwo amuwona kuti Iye anali nayo mphamvu imeneyo. Iwo anamufunsa Iye. Herode anati, “Ndichitire ine chozizwitsa. Ndirole ine ndikuwone Iwe ukuchita chinachake.” Ndipo iye anamupempha Iye kuti adziyankhulire Yekha. Iye anaimea, ngati, wosayankhula pamaso pa omusenga ake, ngati nkhoa yosayankhula pamaso pa oyisenga.

³⁹ Iwo anakulungiza chisanza kuzungulira mutu Wake, tsiku lina, gulu la asilikari otsutsa, ndipo anamumenya Iye pa mutu, ndipo anati, “Tsopano ngati Iwe uli mneneri, ngati Iwe ukudziwa zinthu zonse izi, ndi zina zotero, tiuze ife yemwe wakumenya Iwe. Tichitire ife chozizwitsa.”

⁴⁰ Pamene Satana anakomana naye Iye koyamba, Satana anati, “Tsopano ngati iwe ungandichitire ine chozizwitsa, ine ndikhulupirira kuti Ndiwe Mwana wa Mulungu. Sandutsa miyala iyi ikhale mkate. Ndirole ine ndikuwone Iwe ukuchita izo.”

Yesu anangobwereza Lemba moyankha basi kwa iye.

⁴¹ Ndiyeno, nthawi iliyonse, Satana amafuna kuti azimuwona Iye akuchita chozizwitsa. Anthu omwe ali ogwidwa ndi Satana, amafuna kuti azimuwona Iye, “Ndichitire ine chinachake. Ndirole ine ndikuwone Iwe ukumuchiza *uyu*. Ndirole ine ndikusupule pa dzanja Lako; ndipo Iwe upachize apo ndipo ine ndikukhulupirira Iwe.” Ndi inu apo. Mzimu woipa womwewo umene unati, “Tsikapo pa mtanda tsopano ndipo ife tikukhulupirira Iwe. Manja Ake atakhomeredwa pamenepo. Iwe ukumuitana Eliya; tiyeni timuwone iye abwere, adzakupulumutse Iwe tsopano. Ngati Iwe wapeza chifundo

chochuluka chotero mwa Iye, mwa Mulungu, tiyeko timuwone Iye akukupulumutsa Iwe. Tsika pa mtandapo ndipo ife tikukhulupirira iwe. Chita chozizwitsa pamaso pathu.”

⁴² Zozizwitsa nthawizonse zikhala zikuwadodometsa osakhulupirira. Koma, chimodzimodzibe basi, ngakhalebe, Atate athu Akumwamba ndi Mulungu wochita zozizwitsa. Ndi choncho. Kulikonse komwe Iye wakhala ali, chirichonse chimene utumiki Wake wakhala uli, komwe Iye wakhala ali ndi atumiki Ake, uko kwakhala kuli zizindikiro, zodabwitsa, ndi zozizwitsa.

⁴³ Tsopano Ambuye akudalitseni inu, pamene ine ndikuwerenga nkhani ya mu Lemba pano kwa mphindi zochepa, ndiyeno ife tipita mu utumiki, ndiyeno molunjika ku utumiki wa machiritso.

⁴⁴ Tsopano penyani. Yesu, pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, Iye anati, “Tsopano, zinthu zimene Ine ndikuzichita, inunso muzidzazichita. Zoposa izi inu muzidzazichita, kapena zazikulupo, pakuti Ine ndikupita kwa Atate Anga. Tsopano komabe kanthawi pang’ono,” ine ndikumubwereza Yesu, “komabe kanthawi pang’ono ndipo dziko silimandiwona Ine kenanso, komabe Inu muzindiwona Ine, pakuti Ine ndikhala ndi inu, ngakhale mkati mwanu, mpaka ku mathero a dziko.” “Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.”

⁴⁵ Ndi Akhristu angati muno, usikuuno, mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, kuti Yesu Khristu anawuka kuchokera kwa akufa ndipo ali moyo usikuuno? Tiyeni tiwone dzanja lanu. [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino, ngati Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, kodi Iye sangabale, usikuuno, mu Mpingo Wake, chinthu chomwecho Iye ankachita mu Mpingo Wake, pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, mu thupi? [“Ameni.”] Mukuona? Ndi basi... Mzimu Woyera ndi Mzimu wa Yesu Khristu. Iye ali pano mu mawonekedwe auzimu, wamoyo mochuluka basi monga Iye anali nthawizonse; muno, akukhala mwa ife, kumachita zinthu zomwe Iye ankachita pamene Iye anali kuno pa dziko lapansi, ngati chitsimikizo cha kukhala Kwake ndi ife. “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mkati mwanu, mpaka ku mathero a dziko.” Ambuye akudalitseni inu.

Tiyeni ife tipemphere.

⁴⁶ Atate Akumwamba, usikuuno, pezani ulemerero, Atate Akumwamba, kuchokera mu kuyesetsa kwathu kumene ife tikuyesera kuti tikuyikire kwa ulemerero Wanu. Tsopano pano pali Mawu, pano pa guwa, atatsegulidwa. Koma ndani angawamvetse Iwo? Pamene, Iwo analembedwa mwa kudzodza, zinalonjezedwa, kuti, “Iwo anali obisidwa ku maso a anzeru ndi aluntha, ndipo akanadzamaululidwa kwa makanda omwe angathe kuphunzira.” Tsopano, Atate, ife tikupemphera kuti

Inu mutilole ife tidzitenge tokha ngati makanda, osadziwa kalikonse, kuti ife tikhoze kuphunzira zinthu zina kupyolera mu vumbulutso mwa Mzimu Woyera. Mulole Iye awatenge Mawu a Mulungu tsopano ndipo awapereke Iwo kwa mtima uliwonse monga ife tikuwasowera. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake. Amenii.

Mu Genesis . . .

⁴⁷ Pakungotentha pang'ono pamwamba pano; ine ndikulungalira kuti kuli kumeneko, nakonso. Ngati osamalira pamalo angati atipatse mpweya pang'ono pokha mnyumba muno, kuti anthu amverere bwinoko pang'ono. Ine ndikuwaona ena a iwo akukupiza.

⁴⁸ Tsopano, mu Genesis mutu wa 22, ine ndikufuna kuti ndikokere tcheru chanu ku mawu pang'ono pano; basi pa kutseka kwa msonkhano uno, wa Uthenga. Ine nthawizonse ndimakonda kunena, kapena kuwerenga Mawu ena pano, chifukwa Mawu awa sadzachoka konse. Ndipo Iwo ali Amuyaya, kwanthawizonse.

⁴⁹ Ndipo ngati ine ndikanati ndinene chirichonse cha mutu, wa usikuuno, ine ndikukhumba kuti ndiyankhule pa izi: *Mulungu Alinayo Njira Yoperekedweratu*. Iye alinayo njira yoperekedweratu ya kufikira kwa Iye. Iye alinayo njira ya kuthawira. Ndipo Iye alinayo njira yoperekedweratu pa chirichonse chimene ife tikuchisowa. Ngati ife tingakhoze kokha kuipeza njira iyo yomwe Mulungu waipereka, ndiye ife titsimikiza kuti tizipeza izo. Ngati Mulungu . . .

⁵⁰ Ngati nyumba ino inaperekedwa pano kuti izisamalira, kuti mvula isamafike pa ife; bola ngati ife tilowa mu nyumba muno, ndiye ife tachoka ku mvula.

⁵¹ Ngati Mulungu wapereka njira ya chipulumutso, ife titati taipeza njira yoperekedwa iyo, ife tikhoza kukhala nacho chipulumutso. Ngati Mulungu alinayo njira yoperekedweratu ya machiritso Auzimu, ndiye ife tikhoza kuwapeza, tikapita mu njira imeneyo, ife tipeza machiritso Auzimu. Ngati Iye wapereka mtendere kwa osakhazikika, ndiye ngati ife tilowa mu njira imeneyo ndi kuipeza njira Yake yoperekedwayo, ife tikhoza kukhala nawo mtendere.

⁵² Tsopano kuwerenga kuchokera pa ndime ya 7 ya mutu wa 22. Zindikirani izi tsopano; nkhani yaikulu, ya mwasewero ili pano patsogolo pathu.

Ndipo Isaki anayankhula kwa Abrahamu atate ake, ndipo anati, . . . atate: ndipo iye anati, Ine ndiri pano, mwana wanga. Ndipo iye anati, Taonani moto ndi nkhu: koma alikuti mwanawankhosa wa nsembe-yopsyereza?

Ndipo Abrahamu anati, Mwana wanga, Mulungu adzipatsa yekha mwanawankhosa wa nsembe-yopsyereza: . . .

⁵³ Ambuye atawonjezera madalitso Awo ku kuwerenga kwa Mawu amenewo. Ine ndikhoza kuwerenga, moyankha kwa izo, ndime ya 14, nayonso.

Ndipo Abrahamu anatcha dzina la malowo Yehova-yire: monga izo ziri kunenedwa mu tsiku lino, Mu phiri la Yehova izo zimawoneka.

⁵⁴ *Yehova-yire* linali dzina la Mulungu la chiwombolo. Mulungu, mawu oti *Yehova-yire*, amatanthauza, “Mulungu adzipatsa Yekha nsembe.” “Mulungu akonza njira,” mwakunena kwina. Tsopano, Mulungu anali ndi maina apawiri asanu ndi awiri achiwombolo; *Yehova-yire*, ndi *Yehova-manase*, ndi *Yehova-rafa Mchiritsi*, ndi maina apawiri osiyana onse awa omwe Iye anali nawo, chimene Iye anali, oyimira chomwe Iye anali kwa anthu. Ndipo nsembe yoperekedwa iyi, usikuuno, *Yehova-yire*, “Ambuye adzipatsa Yekha mwanawankhosa.”

⁵⁵ Nkhani yaikulu ya mwasewero yomwe ili patsogolo pathu, pamene—pamene ife tikusunthira umo tsopano, Mzimu Woyera utawatenga Mawu otsatira pang’ono awa ndi kuwumanga mtima uliwonse.

⁵⁶ Tsopano uno ndi usiku wotsiriza wa msonkhano, ndipo ine ndikufuna wina aliyense wa inu kuti mundipatse ine tcheru chanu chosagawanika, ndipo mumvetsere mwatcheru tsopano. Ife tikuyesera kuti tilowemo kwa chigonjetso chachikulukulu cha msonkhanowu. Uno ndi usiku wotsiriza. Kawirikawiri pamakhala anthu ambiri omwe amachizidwa usiku wotsiriza kuposa omwe amakhalapo mu misonkhano ina yonse; kuyembekezera kwakukulu.

⁵⁷ Satana amamenya zolimba. Chirichonse chimapita molakwika, mwakuwoneka, chifukwa Satana akuyesetsa kuti awayike anthu awo mu kumangika, ndi china chirichonse, kotero kuti iye akhoze kuwaika iwo kutali ndi nthawi yaikulu iyi ya kupsyinjika imene tsopano ife tiri kulowamo, kwa chachikulu, monga ife tingati tinene, “Kupita mkati kuti tikaphe tsopano.”

⁵⁸ Iye wamenyedwa kale, ku ngodya. Iye wayalutsidwa kale, ndi machenjerero ake onse ayalutsidwa. Ndipo amuna ndi akazi amuvomereza Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wawo. Anthu okhala ndi khansara ndi zotupa, ndi—ndi china chirichonse, achiritsidwa kale; zonena za madotolo zatsimikizira kuti izo ndi zoono.

⁵⁹ Tsopano pano pali gulu la anthu loterolo muno usikuuno, akhala, akuyembekezera pansu pa kuyembekezera kwakukulu. Ndipo Satana, ngati iye angakhoze kusokoneza malingaliro anu, ndizo zonse zomwe iye ayenera kuzichita. Koma tiyeni tipitemo tsopano ku kupha kwakukulu, pakali pano, kuti

timuthamangitse Satana ndi zimphamvu zake zonse mpaka kunja kwa nyumbayi, kuti Mulungu akhoze kukhala nawo ufulu wa njira ndi kumuchiza munthu wodwala aliynse, kwa ulemmerero wa Mulungu.

⁶⁰ Tsopano, Abrahamu mbadwa anabwera uko kuchokera ku Sinara, kutali ndi nsanja ya Babulo. Iye ndi abambo ake anayenda mpaka kukalowa mu z—zigwa. Ndipo uko, Abrahamu, pa usinkhu wa pafupi zaka sevente-faifi, Mulungu anamuitana Abrahamu, mwa kusankha, ndipo anamutumiza iye kunja kwa dziko lake lomwe, anamuza iye kuti akanati adzakhale ndi mwana mwa mkazi wake, Sarah, yemwe anali usinkhu wa zaka sikisite-faifi pa nthawiyo. Mulungu analonjeza. Ine ndikufuna kuti inu muwone momwe malonjezo a Mulungu aliri enieni kwa iwo omwe angawalandire iwo. Ndipo Iye anamuza iye zomwe Iye akanati azichite. Ndipo iye anamusamutsako, asakudziwa komwe iye anali kupita, koma kumakayenda mu dziko lachirendo.

⁶¹ Mulungu, pamene Iye awaitana anthu, Iye amawaitanira ku kudzilekanitsa kwathunthu kwa zinthu zonse za mdziko; kutheratu psyiti ku zinthu zachidziko. Dzimatuleni nokha, ndipo Mulungu akudalitsani inu. “Tulukani pakati pawo; musakhale ogawana nawo za machimo awo.” “Musadzimange nokha gori pakati pa osakhulupirira, koma mudzimange gori ndi okhulupirira, mbadwa limodzi za Ufumu.”

⁶² Ndipo Abrahamu anayenera kuti amutenge mkazi wake ndi kuchoka mdzikolo. Koma iye anamukhulupirira Mulungu, mwa chikhulupiriro. Iwe sukanakhoza kuzilingalira izo. Palibe njira yopezera momwe iye akanakhozera kuchita izo konse. Momwe, mkazi uyu, anakhallira ndi iye kuyambira ali msungwana wamng’ono; onse awo, aang’ono, anthu athanzi, masiku onse awa; mpaka iye analino forte, fifite, sikisite, mwinamwake zaka twente-faifi atadutsa kusintha kwathupi. Ndipo Mulungu anati, “Iwe udzakhala ndi mwana mwa mkazi uyu.” Ndipo Abrahamu anamukhulupirira Mulungu; motsutsana ndi kulingalira konse, motsutsa kufufuza konse kwa sayansi, ngakhale mpaka ku tsiku lino. Zingatheke bwanji kuti mkazi, wasinkhu wa zaka sikisite-faifi, kukhala naye mwana? Koma Mulungu anati iye akanati adzachite izo, koteru Abrahamu anazikhulupirira izo.

⁶³ Chotero iye anapita uko, asakudziwa kumene iye anali kupita. Ndipo, potsiriza, Sarah atafika pokhala ali pafupi usinkhu wa zaka handiredi, Abrahamu anali akukhulupirirabe. Ine ndikufuna kuti inu muziwone izo. Akukhulupirirabe kuti Mulungu anali woti asunga lonjezo Lake, iye anali nazo zonse zokonzekera mwanayo. Ndipo potsiriza mwanayo anafika. Mulungu nthawizonse amachita izo mwa njira imeneyo. Iye anamubweretsa mwanayo mu nyengo yake basi.

⁶⁴ Onani, pamene zimatalikira talikira, Abrahamu analingalira, “Chabwino, ine sindinamulandire iye lero. Ine sindinamulandire iye mwezi uno. Ine sindinamulandire iye mwezi watha. Koma zinalibe kanthu kuti zatalika bwanji, momwe zikuchedwera, ndi pamene ine ndikufika pakukalambira, ndi mochulukira momwe chiti chidzakhale chozizwitsa.” Mpatseni Mulungu matamando pa izo.

⁶⁵ Mmalo moti azifooka, monga ife tingakhale tiri; kupemphereredwa, usikuuno, ndi k—kuchiritsidwa; titi nkudwalika mawa, inu nkuti, “O, chabwino, munalibe kanthu mu izo.” Ndicho chifukwa; inu simukhoza kuwasunga Mawu a Mulungu.

⁶⁶ “Mawu Anu ine ndawabisa mu mtima wanga, O Ambuye!” Davide! Abiseni Mawu a Mulungu mu mtima mwanu, ndiyeno Mulungu awasunga Mawu amenewo. Mulungu ayenera kumasunga Mawu Ake. Mulungu sasowa kuti azichiza, kuti atsimikizire mphamvu Yake. Koma Iye amayenera kumachiza, kuti asunge Mawu Ake. Ndiko kulondola. Mulungu samasowa kuti atsimikizire kalikonse. Iye ndi Mulungu. Koma chimene Iye amayankhula, Iye amakakamizidwira ku Mawu Ake. Kotero muli inu ndi ine okakamizidwira ku mawu athu. Ndipo Mulungu ndi wokakamizidwira ku Mawu Ake.

⁶⁷ Chotero ngati machiritso Auzimu ali mu Mawu, izo zikhazikitsa icho. Ngati “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa,” imeneyo inali nsembe, izo zikukhazikitsa icho. Momwe ine ndikudziwira, ndizo zonse. Ngati Mulungu anachita izo uko, analonjeza kuti Iye akanamadzachita izo, izo zikukhazikitsa icho.

⁶⁸ Umo ndi momwe izo zinaliri ndi Abrahamu. Zinalibe kanthu zomwe zimabwera kapena zimapita, Abrahamu anakhulupirira izo mulimonse. Mwinamwake anali nazo zonse zokonzekera mwanayo, ndiye Mulungu anamulola kuti iye apite mpaka iye anafika usinkhu wa zaka handiredi; anamusandutsa iye ndi Sarah kubwerera wa msungwana, mnyamata kachiwiri, ndipo anawapatsa iwo mwana.

⁶⁹ Apo, chithunzi chake chokongola tsopano chimene ife tiri nacho patsogolo pathu, choti tichilingalire. Ndi uyu mwanayo, akudzakhala pafupi usinkhu wa zaka sikisitini, seventini, mtima womwe wa nkhalamba yaimuna iyi ndi yaikazi; wokondedwa, kamunthu kakang’onoko.

⁷⁰ Tsopano Mulungu akuyankhula ndi Abrahamu, usiku wina, anati, “Abrahamu, umutengere iye pamwamba apo ku phiri, ndipo ukamupereke iye uko. Ukamuphe iye.” Ndipo, komabe, Mulungu anali atamulonjeza Abrahamu, kuti, “Kupyolera mwa Isaki mafuko onse a dziko akanati adzadalitsidwe.” Iye azichita chotani tsopano, pambuyo pa kuyembekezera kwa zaka zonse

izi, akukhulupirira; ndipo tsopano pambuyo pa nthawi yonse iyi, zitheka motani mwana . . . Chiyembekezo chokha cha lonjezo la Mulungu, ndipo Mulungu anamuuza Abrahamu kuti awononge chiyembekezo chirichonse chomwe iye anali nacho apanso.

⁷¹ Mukuona momwe Mulungu amachitira? Kuyesa! Mulungu amakulola iwe nthawizina kuti udwalike pang'ono utapemphereredwa kale, basi kuti akuyese iwe. Kuyesa ndi mayesero a chikhulupiriro! Koma, “iye yemwe apirira.” Ndi izo apo. Gwiritsitsanibe; mutengeni Mulungu pa Mawu Ake. Khulupirirani Mawu aliwonse a Iwo. Ziribe kanthu zomwe china chirichonse chinena kapena chichita; khulupirirani Izo, mulimonse. Ziribe kanthu momwe zochitika zikuwonekera; mukhulupirireni Mulungu, mulimonse.

⁷² Ndiye, apo Mulungu anati, “Umutenge mwanayo ndipo umutengere iye pamwamba apo. Ine ndati ndidzalidalitse dziko lonse ndi iye. Iwe wayembekezera kwa zaka zonse izi; tsopano iwe uli usinkhu wa zaka handiredi, pafupi usinkhu wa zaka handiredi ndi sikisitini, eyitini. Tsopano Ine ndikufuna iwe umutenge mwana wamng'onoyo, ndipo umutengere iye pamwamba pa phiri uko ndipo ukamuphe iye.”

⁷³ Mai, o, zinawoneka zachirendo kwambiri, zosalingalirika, kuti Mulungu akanamufunsa Abrahamu kuti amuwononge mwana wake yekhayo. Koma, kuseri kwa izo tsopano, ife tikuchiwona chithunzi chomwe Iye anali kuchijambula; Mulungu kumupereka Mwana Wake yekha.

⁷⁴ Abrahamu sanafune kuti awauze amake, ndithudi, izo zikanaswa mtima wake. Anaika zishyalo abulu ena, ndipo anawatenga antchito angapo, ndipo anakwera napita ku phiri.

⁷⁵ Ine ndimangolikonda gawo ili apa. Ndiye iye anakafika kumene phirilo linali, ndipo iye anati kwa wantchito, “Inu mutidikire pano tsopano, pamene mwanayu ndi ine tikupita kutsidya kuti tikapembedze. Ndipo mwanayu ndi ine tikabwerera.”

⁷⁶ Akabwerera chotani iyeyo, pamene iye akupita kuti akamuphe iye? Koma Abrahamu ankadziwa ichi, kuti, “Iye anali atamulandira iye mwa chiwerengero, ngati wina wochokera kwa akufa, ndipo Mulungu anali wokhoza kumuutsa iye kwa akufa.” Mulungu akanadzapanga njira yothawirapo, mwanjira yina. Motani, iye sanali kudziwa. Mulungu anamuuza iye, umutenge iye ndipo ukamuphe iye, ndipo icho chinali chinthu chake chokha chimene iye anali woti achichite.

⁷⁷ “Inu mutidikire pano. Mwanayu ndi ine tikupita kutsidya kuti tikapembedze, ndipo mwanayu ndi ine tikabwerera.”

⁷⁸ Zindikirani, Isaki wamng'ono ananyamula nkhuuni, anapita pamwamba pa phiri. Abambo ake, akutsogolera; Isaki, pambuyo, ali ndi nkhuuni pa nsana wake. Tayang'anani pa izo, chithunzi chokongola cha zaka zina eyiti handiredi mtsogolo,

Mulungu akumutsogolera Mwana Wake Yemwe waku Kalvare, ali ndi nkhuuni pa nsana Wake, kukachita nsembe. Chithunzi, Mulungu akukonza njira yothawirapo.

⁷⁹ Tsopano, ndipo pamene Abrahamu anafika pamwamba pa phiri, anaigudubuzira miyala palimodzi ndipo anamanga guwa, anaika nkhuuni pansu; kamwana kakang'onoko kanati, "Atate?"

Iye anati, "Ndine pano, mwananga."

⁸⁰ Iye anati, "Guwa ndi ili, ndipo nkhuuni ndi izi, koma alikuti mwanawankhosa wa nsembe?"

⁸¹ Ndipo Abrahamu, ndi liwu lonjenjemera, anati, "Mulungu apereka mwanawankhosa wa nsembe." Tayang'anani pa mphindi ya mdima iyo. Komabe, chikhulupiro, chosakanizidwa, sichikanamulola iye kusamukhulupirira Mulungu. Zindikirani. O, ine ndimangoyang'ana pa nkhuuni iyi nthawizina ndi kulira mwa chisangalalo.

⁸² Abrahamu anamanga manja a mwana wake yemwe, anamugoneka iye pa guwa; anasolola mpeni kuchokera pa lamba wake, ndipo anali atakonzeka kuti achotse moyo wa mwana wake, chifukwa Mulungu anali atamuuzwa iye kuti achite choncho.

⁸³ Ndipo pa nthawi imeneyo, Liwu linafuula kuchokera Kumwamba, linati, "Abrahamu, imitsa dzanja lako!" Ndipo pamene Mzimu Woyera unagwira dzanja lake, anati, "Ine ndawona kuti sunamukanize mwana wako yemwe. Ine ndikudziwa iwe umandikonda Ine."

⁸⁴ Ndipo cha mu nthawi yomweyo, chinachake chinayamba kulira uko mu chipululu, chitagwidwa pamwamba pamenepo, ndipo apo panali kamwana kankhosa. Mulungu anapereka nsembe.

⁸⁵ Penyani, "mwanawankhosa." Iyo inkayenera kuti ikhale nkhuuni, yamphongo, mwanawankhosa. Choimira cha Khristu, Yemwe akanadzatenga malo a imfa. Ndi imeneyo Nsembe yoperekedwa ndi Mulungu. Ndipo Abrahamu anaipereka nsembeyo mmalo mwa Isaki. Kukongola kwake kwa chithunzichi tsopano! Zindikirani, Mulungu nthawizonse ankakonza njira. Iye akonza njira, usikuuno, kwa wina aliyense wa inu.

⁸⁶ Ndipo Israeli, pamene iwo anali uko mu Igupto, iwo anali mu msinga ndi mu vuto, ndipo iwo anayamba kulirira kwa Mulungu kuti awaombole. Zindikirani, njira yomwe Mulungu adzaipereka ndi pamene ife tiri mu Mawu a Mulungu. Israeli anali nao Mawu a Mulungu kuti iwo akanati adzatulukeko uko, tsiku lina. Chotero, iwo anayamba kulirira kwa Mulungu, molingana ndi chifuniro cha Mulungu, kuti Mulungu apereke zomwe Iye anali atalonjeza kuti adzazichita.

⁸⁷ Ndi inu apo. Inu mukamapempherera chinachake chomwe chiri kunja kwa chifuniro cha Mulungu, inu simungakhoze kukhala ndi chikhulupiriro kwa icho. Koma pamene Mulungu alonjeza chirichonse, ine ndimakhulupirira kuti Iye asunga Mawu Ake. Chotero, iwo ankadziwa.

⁸⁸ Ndicho chifukwa Abrahamu anadziwa kuti Mulungu akanati amuwombole iye, mwinamwake, chifukwa Iye anali atalonjeza izo kupyolera mwa Isaki, mafuko onse mu dziko akanati adzadalitsidwe.

⁸⁹ Ana a Israeli, uko mu Igupto, iwo ankadziwa kuti Mulungu anali atawalonjeza iwo chiwombolo, chotero iwo anapita namakapempherera lonjezolo.

⁹⁰ Inu mukuti, “M’bale Branham, ngati ine ndikanamadziwa machiritso Auzimu, kuti Mulungu anali atalonjeza izo!”

⁹¹ Chabwino, tiyeni tizitenge izo mphindi yokha, Yakobo 5:14. Ngati kulibe msonkhano wokopa wa machiritso mu mzinda kwina wake, iye anati, “Ngati alipo wina pakati panu, akudwala, iyeyo ayitane akulu a mpingo; awadzoze iwo ndi mafuta, ndi kuwapempherera iwo. Pemphero la chikhulupiriro lidzamupulumutsa wodwala.” Ndiwo Mawu a Mulungu, njira yoperekedwa ndi Mulungu. Ndiko kulondola.

⁹² Zindikirani pamene Israeli anayamba kulira. Mulungu anayamba kumva, ndipo anapereka njira yothawirapo; anamutumiza Mose kwa iwo. Zinali zodabwitsa bwanji izo, atalirira kale chiwombolo; ndipo pamene chiwombolo chinabweretsedwa kwa iwo, iwo analephera kuchizindikira icho, ndipo anachikana icho, ndipo anachita kuvutikira zaka forte zina.

⁹³ Kodi izo si zenizeni za lero? Mulungu akakubweretserani inu chinachake, ndipo mumawopsyedwa nacho.

⁹⁴ Mulungu anatumiza Mzimu Woyera kwa inu anthu omwe simunkawukonda mpingo wonse wachizolowezi uwu, chipembedzo cha zamipingu. Mulungu anakutumizirani inu Mzimu Woyera; magulu aakulu awo akuwopsyedwa ndi Iwo.

⁹⁵ Ophunzira anali pafupi kuti amire, usiku wina, mu ngalawa yaing’ono, ndipo iyo imapendekeka pa nyanja, ndipo iwo anali akulirira chithandizo. Ndipo pamene iwo anamuwona Munthu yekha yemwe akanakhoza kuletsa mafunde, akubwera, iwo anachita mantha ndi Iye ndipo ankaganiza kuti Iye anali muzukwa. Chiyembekezo chokha chomwe iwo anali nacho; iwo analikuwopsyedwa ndi Icho.

⁹⁶ Alipo amuna ndi akazi akhala pano usikuuno, ali ndi khansara, vuto la mtima, matenda owopsya, mopanda kukaika. Ndipo chiyembekezo chokha chomwe inu muli nacho... adokotala anu atachita kale—atachita zonse zomwe iwo

akanakhoza kuzichita. Inu mwangokhala amantha kuti mufikire apo ndi kumudalira Iye.

⁹⁷ Musati muzichita mantha. Atengeni Mawu Ake. Imani apo pomwe. Ndi njira yoperekedwa ndi Mulungu kwa inu. Mulungu wakutumizani inu kuno, usikuuno, pa cholinga chimenecho. Iye sanakutumizeni konse inu kuno, usikuuno, kuti ine ndikupempherereni inu. Iye wakutumizani inu kuno, usikuuno, kuti muilandire njira Yake yoperekedwa, Yesu Khristu Nsembe yotetezera kwa tchimo ndi matenda. Ine ndikuyembekeza inu mukumvetsa izo.

⁹⁸ Zindikirani, iwo ankalirira chiwombolo. Mulungu anawatumizira iwo chiwombolo. Iwo anachita kuyembekezera zaka forte kachiwiri kuti azilandire izo.

⁹⁹ Mu chipululu, Mulungu analonjeza kuti Iye akanamapereka zonse zomwe iwo anali kuzisowa. Iwo mkate unawathera. Ndipo Yehova-Yire yemweyo, “Mulungu apereka nsembe,” kwa Abrahamu; zaka foro handiredi mtsogolo, anali akadali Yehova-Yire, kuti apereke chirichonse chomwe ana Ake anali kuchisowa.

¹⁰⁰ Ndi izi pano. Ine ndikufuna izo zipite patali mwakuya ku mbali ya kumanzere, pansu pa nthiti yachisanu. Mvetserani. Iye akadali Yehova-yire, nsembe yoperekedwa ndi Ambuye. Ilandireni Iyo. Musati muzingoyesera kuzilingalira izo. Musati muziyesera kuzilingalira; inu simungakhoze kuzilingalira. Njira za Mulungu ndi zopitirira kuzifufuza. Inu simumamulingalira Mulungu. Inu simumamudziwa Iye mwa chidziwitso. Inu simumamudziwa Iye mwa maphunziro. Inu mumamudziwa Iye mwa chinthu chimodzi chokha, chikhulupiriro. Inu simungakhoze kulingalira. Ndi zosalinalirika kukhulupirira kuti inu mungakhoze kuzilingalira izo. Inu simungakhoze. Inu mumangoyenera kuzivomereza izo.

¹⁰¹ Zindikirani, kachiwiri, mu nthawi yaikulu, yopambana iyi. Mkate unawathera. Kodi iwo akanatani? Ngati Mulungu anawauza iwo anali kupita ku dziko lolonjezedwa, ziri kwa Mulungu kuti awasamalire iwo mpaka akafike uko. Ndipo Yehova-Yire yemweyo anali apo ndi iwo. Ndiyeno pamene iwo mkate unawathera, Yehova-Yire anapereka njira ya mkate, njira yonse kudutsa mu chipululu. Manna ankavumba kuchokera kumwamba.

¹⁰² Iwo madzi anawathera. Ncha ntchito yanji kumadandaula? Yehova-yire, nsembe yoperekedwa ndi Ambuye, inali apo ndi iwo. Ndipo iye analikantha thanthwe. Ndipo iwo ankayankhula kwa ilo, kuyambira apo mpakana, ndipo madzi ankatuluka mochulukuka. Kumwetsera ng’ombe zawo zonse, zikwi za magaloni pa mphindi, akutsanuliridwa kuchokera mu thanthwe la mu chipululu chouma. Nzosalinalirika, si choncho? Koma Mulungu anawapereka. Inu simumalingalira momwe Iye

amachitira izo. Iye amangozichita izo chifukwa Iye anati Iye akanadzatero.

¹⁰³ Akanakhoza bwanji wodwala, atagona, akufa ndi khansara, madokotala opambana atanena kuti palibe chiyembekezo konse, iwo akanakhoza bwanji kuchiritsidwa? Ndi zosalinalirika. Koma Iye ndi Yehova-Yire, nsembe yoperekedwa ndi Ambuye. Ndi zokongola bwanji!

¹⁰⁴ Tsiku lina, iwo anakhala ndi matenda mu msasa. Iwo analibe, mwina, opanda adokotala ndi chisamaliro. Omwe anali... Mose kunjira uko ndi gulu lonse lija la anthu, pafupi thuu milioni a iwo, okalamba ndi aang'ono, ndi odwala ndi onse; pamene iwo ankatuluka mu chipululu, uko kunalibe wofooka mmodzi pakati pawo. Koma tsopano zindikirani pamene iwo anali kunjira uko, ndipo iwo ankachimwa, ndipo njoka zinayamba kumawaluma iwo, panalibe kanthu komwe iwo akanakhoza kuchita. Ndipo Mulungu, ndi pamene iye Mose amayankhula ndi Iye, anapereka chitetezero; anamuza Mose, "Pita ukatenge chidutswa cha mkuwa. Ukapange njoka kuchokera mwa iwo, ndipo ukayiike iyo pa mtengo. Ndipo kudzachitika, yense yemwe adzayang'ana pa njoka iyi adzachiritsidwa."

¹⁰⁵ Choimira chokongola, kachiwiri. Mkuwa, njoka payokha, inkayankhula za tchimo loweruzidwa kale; Eteni, pamene Mulungu analengeza chiweruzo pa njoka, iyo inali itaweruzidwa kale.

¹⁰⁶ Mkuwa umayankhula za chiweruzo Chauzimu, pa guwa la mkuwa pamene matupi azinyama anali kuwotchedwa. Magazi atatengedwa kale; naini koloko iliyonse mmawa, thwelofu koloko, ndi firii koloko madzulo, magaloni a magazi ankaponyedwera pa guwa ili, pa matupi a nyama zakufa, utsi wakuda unkakwera mmwamba. Myuda aliyense mu Palestina ankagwada pa maondo ake, ndi manja ake kuloza Kumwamba; ndipo, pamene utsi uwo unkakwera mmwamba, mapemphero ake ankapita limodzi nawo. Chabwino. Chiweruzo Chaumulungu; matupiwu ankaotchedwa pa guwa la mkuwa.

¹⁰⁷ Basi monga mu Israeli, pamene Ahabu anapangitsa Israeli kuti achimwe. Ndipo Eliya anatuluka kuti akayang'ane mu mlengalenga; zaka zitatu ndi miyezi sikisi, kopanda mvula. Iye anati, "Mukuwoneka ngati mkuwa," chiweruzo Chaumulungu.

¹⁰⁸ Mu Chivumbulutso, pamene iwo anamuwona Yesu, mu Chivumbulutso 1, "Mapazi Ake ankawoneka ngati mkuwa," chiweruzo Chaumulungu.

¹⁰⁹ Njoka inkayankhula za chiweruzo Chaumulungu, ndi kuti amusangalatse Mulungu. Ziweruzo zake ndi Zaumulungu. Ndipo, ndiye, mtengowo unkaimira mtanda. Ndipo njoka inkaimira Yesu, Ambuye Yesu okondedwa; Iye anabwera pansu ndipo anapangidwa tchimo. Mulungu Mwiniwake anadziulula Yekha mu thupi, anapangidwa monga mwa thupi lochimwa, kuti

adzachotse matenda ndi tchimo pa dziko lapansi. Ndi zokongola bwanji! Mmenemo Iye anakonza njira. Yesu anati, “Monga Mose anakweza mmwamba njoka ya mkuwa mu chipululu, chotero ayenera Mwana wa munthu kuti akwezedwe mmwamba.”

¹¹⁰ Tsopano kodi njoka ya mkuwa inkakwezedweranji mmwamba? Kwa chifukwa chapawiri. Iwo anali atachimwa ndipo anali kudwala. Tsopano, ndiye, Yesu anakwezedwa mmwamba, “anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu; ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa,” chifukwa cha pawiri. Ndipo izo zikadali zenizeni basi, usikuuno, kuti Khristu azichiza odwala, monga izo ziliri kuti azipulumutsa ochimwa.

¹¹¹ Nchozizwitsa mochuluka kuti Iye apulumutse wochimwa; Iye ayenera kuti amusinthe njira zake. Ndipo, ndithudi, iye atamusintha kale, iye akanati azidziwa momwe angati azimukhulupirira Mulungu pa machiritso ake. Mukuona zomwe ine ndikutanthauza?

¹¹² Choimira china chokongola, mwamsanga, ine ndinapezeka ndikuganizira, mu Bukhu la Rute. Ambiri a inu mumathamanga pamwamba pa Bukhu limenelo; popanda kuganiza, osaganiza chomwe ilo liri. Ndiyo imodzi ya nkhani zazikulu kwambiri mmenemo, ya choimira cha Khristu, mu Chipangano Chakale chonse.

¹¹³ Mu mutu woyamba wa—wa Bukhu la Rute. Naomi, mawu oti *Naomi*, amatanthauza “wokondweretsa.” Iye, mwamuna wake, ndi ana ake aamuna awiri, anachoka ku Palestina, choimira mpingo. Ndipo iwo anachoka ku Palestina, anapita uko mu dziko la Moabu. Ndipo uko iwo anakakhala, atachoka ku dziko la kwawo. Ndicho chophiphiritsa cha kubwerera mmbuyo, monga Israeli anachitira. Myuda aliyense yemwe ankachoka ku Palestina anali kunjwa kwa chifuniro cha Ambuye. Mulungu anapereka Palestina kwa Ayuda, ndipo anati, “Muzikhala muli mmenemo.” Ndipo Rute anatuluka . . . kapena, osati Rute, koma Naomi.

¹¹⁴ Ndipo ana ake aamuna awiri anakwatira. Ndipo amuna onsewo anafa; mwamuna wake ndi ana aamuna awiri. Iye anawuyamba wobwerera kwawo. Azipongozi ake aakazi anapita theka la ulendo ndi iye. Mmodzi wa iwo anakweza maso ake ndipo anayang’ana mmbuyo ku dziko lakwawo; iye anabwerera. Koma Rute, wa Chimoabu, iye sakanakhoza kupita. Iye ankawakonda apongozi ake.

¹¹⁵ Iye anati, “Bwerera kwa anthu a kwanu. Ine ndakalamba. Ndipo ngati ine nditati ndidzakhale nawo ana ena, bwanji, . . .” Inu mukudziwa malamulo, kuti momwe zimayenera kuti zikhalire mu masiku amenewo, inu masikolala a Baibulo. Anati, “Ngati ine ndikanati ndidzakhale ndi mwana, izo zikanati. . . iwe ukanadzakhala wamkulu kwambiri kwa iye

pamene iye akanati adzakule. Chotero bwerera, ndipo ukhoza kukakwatiwanso.” O, ine ndikuzikonda izi.

¹¹⁶ Naomi, tsopano, woimira kwa mpingo wa Chiyuda. Rute, woimira wa Mpingo wa Amitundu. Zindikirani. Ndipo tsopano, pano iye akubwereranso, onani.

¹¹⁷ Rute, pokhala Wamitundu, wopembedza wachikunja, iye anayang’ana mmbuyo ndipo iye anati, “Ine ndipita nanu. Kumene inu mukakhala, ine ndikakhala. Kumene inu mukafera, ine ndikafera. Kumene inu mukaikidwa, ine ndidzakaikidwa. Mulole Mulungu wanu akhale Mulungu wanga.” Umenewo ndi Mpingo Wamitundu ukulandira chipulumutso kupyolera mwa Yesu Khristu Ambuye wathu. Zindikirani chithunzi chake chokongola! Ndipo tsopano ndikukhumba ife tikanakhala nayo nthawi.

¹¹⁸ Mutu wa 2, mu Rute, akuwulula nthawi yake kuti abwerere, pamene iye anabwerera mu nthawi yokolola basi, nyengo ya barele. Ndipo pamene iye anapenya, atayang’ana ku dziko la kwawo, iye analira, “Ine ndimangopukwa kuti ndidzafike mu Palestina!” Mwaona, iwo anali akulira pamene iwo analiwona dziko la Kwawo.

¹¹⁹ Ayuda awo, mwa masauzande, akukhuthukira mu Palestina. Ndiyo kalendara ya lero, m’bale.

¹²⁰ Ine ndikukuuzani inu, ife tikukhala pa mapeto a mseu. Ine sindikanakhala wodabwitsidwa pang’ono kuti alipo anthu ambiri omwe akhala muno, mu usinkhu waukalamba, adzaiwona nthawi pamene sipadzakhala mwala umodzi wosiyidwa pa umzake, mu Louisville, Kentucky. Izo zikhoza kukhala mu chaka china. Ine sindikudziwa; musati munene ine ndinati chaka. Ine sindikudziwa; palibe wina akudziwa. Koma ife tiri pa mapeto a msewu. Ine ndikudziwa izo. Mabomba a haidirojini awo ndi zinthu ziri zokonzeka kuti ziphulike, nthawi iliyonse.

¹²¹ Ayuda akubwerera ku Yerusalemu. Ndipo nyenyezi ya nsonga sikisi ya Davide, mbendela yakale kwambiri mu dziko, ikuwuluka uko mu Yerusalemu, nthawi yoyamba kwa zaka zikwi ziwiri. Chizindikiro cha nthawi!

¹²² Ndipo, zindikirani, chimodzimodzi monga Naomi, yemwe anataya zonse zomwe iye anali nazo, ndipo anali akubwerera basi mu nthawi ya barele.

¹²³ Ndipo Palestina, lero, akuyamba kufutukuka ngati rozi. Zinthu zina zazikulu kwambiri zomwe zikupezeka, chuma cha maiko onse mdziko; mankhwala, akupezeka mu Nyanja Yakufa, ndi opanda mtengo woti nkuutchula. Palestina, dziko lalikulu kwambiri la zipatso; mandimu omwe amalemera mapaundi faifi limodzi, pafupifupi, amalimidwa kumeneko. Taganizani za izo, zonsezo zikukwaniritsa Mawu Aumulungu a Mulungu! Akupita kwawo, Ayuda, akubwerera mu nyengo ya barele!

124 Iye anakweza mmwamba manja ake ndipo analira. Ndipo iwo anati, “Apa akubwera Naomi.”

125 Iye anati, “Musati muzinditcha ine Naomi, pakuti Mulungu wachita nane mowawa,” asakudziwa yemwe iye anali kubwera limodzi naye. Ayuda akudziwa mochepa kuti kumukana kwawo Yesu kunangwapatsa Amitundu malo oti alowelemo. O, ine ndikungozikonda izo. Zindikirani, ndiye, pamene iye anakweza apo maso ake, ndipo analira.

126 Ndipo zindikirani, ndiye iwo ankayenera kuti atenge... Cholandira chake chonse chinali chitalandidwa kwa iye, kotero iwo ankayenera kuti akhale amoyo. Rute, pokhala mkazi wamng’ono, wokongola, anapita ku minda uko ya Boazi, kukakunkha. Izo ndi zomwe osauka ankachita; osowa.

127 Ndikufuna kuti inu muzindikire chomwe oyimira Mpingo ali. Ndi Mpingo wosauka. Rute, pokhala woimira Mkwatibwi Wamitundu tsopano, iye ankapita mmbuyo mwa okolola, kuti azikatola tingala pang’ono tomwe tinali ndi tirigu wina pa ito; kutikunthira ito monga choncho, mu thumba, kuti akhale moyo. Kukunkha, wosavala nsapato, mminda ya a Boazi.

128 Ndipo Boazi anali bwana wa kukolola, kuimira Yesu Khristu Mwana wa Mulungu, zindikirani, Mbuye wamkulu wa kukolola. Ndipo iye anatulukira, kuti adzayang’ane pa minda yake. Iye anawawona okunkha kumeneko; iye anawaona okolola. Ndipo pamene iye anaponyera maso ake cha kwa Rute, iye anagwera mu chikondi naye; Khristu, ndi Mpingo Wake.

Iye anati, “Ndi ndani buthu ili lomwe likukunkha mmundamo?” Iwo anati, “Rute. Anabwera naye pobwera.”

129 Mpingo wa Chiyuda, pansu pa kutsogolera kwa Lawi la Moto, pansu pa kutsogolera kwa Yehova, unakonzana njira, ya Chipangano Chakale, kwa Mkhristu wa Mzimu Woyera wa Chatsopano. Anabwera Naye limodzi nawo. O, ife tikanakhala ndi nthawi kuti tipume pa izi pang’ono pokha, zindikirani, kubwerera.

130 Ndiye iye anati, “Mpangitseni iye abwere ndi kudzakhala pansu pa mthunzi, ndi kudzadya chakudya chatu china nafe.” O, ngati ife tikanakhala nayo nthawi yoti tiyike kutsimikizira kwina pa izo.

131 Zindikirani, ndiye, Boazi anayang’ana pa iye, anawona kuti iye anali “mkazi wangwiro.” Icho ndithudi chiyenera kuti chinali *chiyero*. Chotero iye anayendera chauko ndipo anati kwa okolola onse, iye anati, “Tsopano, inu, pamene dona wamng’ono uyu azibwera mmbuyo mwanu,” musalole kuti iye adziwe izo, anati, “koma tsopano pamene iye azibwera mmbuyo mwanu, kamodzi mu nthawi, muzigwetsa zowonjezera zodzaza mdzanja kuti iye azizitenga izo.” O, mai!

¹³² Kupita cha kumeneko, kukhala ndi ka msonkhano kakang'ono cha *apa*, ndi msonkhano wa pemphero wa nkakhumbi, kusekedwapo, kunyozedwa ndi ena, okunkha ena. Kutola timasache pano ndi apo, ndi kumatipuntha ito. Kupeza mdalitso pang'ono pano, ndi kuyendetsa maora fifite kukapeza wina. Koma ndine wothokoza kwambiri chifukwa cha zokwana mdzanja lalikulu, kamodzi mu nthawi, Mpingo waung'ono wobadwa kachiwiri umazipeza mu chitsitsimutso cha kachitidwe kachikale, zodzaza mdzanja.

¹³³ Iye anazitola izi apo, ine ndikulingalira, nati, “Ambuye adalitsidwe.” Anazipunthamo izo. Ndipo pa nthawi yausiku iye anali nazo zodzaza thumba.

¹³⁴ Boazi, kuimira Khristu, akupita ku mzinda, mwamsanga. Iye sankafuna msungwana uyu kuti apite kwina. Anati, “Kodi iye ndi wandani?”

Anati, “Naomi.”

¹³⁵ Ndipo mpingo wa Chiyuda wa Orthodox unabala Mpingo wa Amitundu. Ndiko kulondola.

Anati, “Iyeyo ndi ndani?”

Anati, “Iyeyo ndi Naomi.” Kotero iye akupita . . .

¹³⁶ Ndiye iye akupita uko. Iye anati, “Tsopano, ine ndiyenera kuti ndiwombole za iye zonse.” Tsopano, lamulo la chiwombolo, mu Chipangano Chakale, nkuti amayenera kukhala wowombola wapachibale. L—lamulo linkafuna, sikuti munthu aliyenera akanakhoza kuombola munda wotaika, koma ankayenera kukhala ali winawake yemwe anali wapachibale; ndiyeno winawake yemwe anali wokhoza kuombola, wolemera mokwanira kuti awombole, wokhoza mwachuma.

¹³⁷ Ndi zokongola bwanji! O, mai! Khristu, wolemera, wolemera pawiri! Mfumu ya Kumwamba, powuona Mpingo waung'ono, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, amagwetsera zodzaza dzanja pang'ono apa ndi apo.

¹³⁸ Zindikirani, njira yokha yomwe Mulungu akadakhoza kuombolera, Mulungu anachita kubwera pansi ndi kudzapangidwa wapachibale kwa ife. Mulungu anali mu Mzimu. Mulungu anabwera pansi ndipo anadzapangidwa thupi. “Mulungu anali mwa Khristu, akuliyanjanitsa dziko kwa Iyemwini.” Ndiye, pofuna kuti amuwombole munthu, Iye anachita kudzakhala munthu, wapachibale. Kodi inu mungakhoze kulingalira Umulungu utabwera pansi, nupangidwa thupi? Chikondi!

¹³⁹ Mnyamata akanamuchitira chiani mkwatibwi wake wamng'ono yemwe akumufuna kuti akhale wokomamtima? Iye ndi wakhungu. Iye angachite chirichonse. Inde, bwana. Iye akumufuna iyeyo. Palibe kanthu kangamuletse iye; iye akhala naye.

140 Umo ndi momwe Mulungu anachitira pamene Iye anauwona Mpingo. Iye anawukonda Iwo. Panalibe kanthu kakanati kamuletse. Iye anali wokonzeka kuti apereke moyo Wake, ndipo Mulungu anasunthira pansu mu thupi la mnofu. Woyenera, Mfumu ya Kumwamba, anakhala wapachibale. Ndiye, Mulungu, Iye atabwera kale mu thupi, mwa Yesu Khristu, anadzakhala Wowombola wapachibale.

141 Mpenyeni Boazi. Tsopano, iye asanati amutenge iye, iye anayenera kuti afunse ngati analipo winawake, wapachibale wapafupi, yemwe akanati azitenge izo, kumutenga iye. Kotero pofuna. . . Kunalibeko aliyense yemwe akanakhoza kuchita izo, kotero ndiye iye anayenera kupanga umboni wapagulu pamaso pa Israeli, kuti iye anali atamuwombola Naomi. Ndipo iye anamuwombola Naomi, pofuna kuti amutenge Rute. O, mai!

142 “Iye anadza kwa Ake omwe, ndipo Ake omwe sanamulandire Iye ayi.” Koma iye ankayenera kuti amuwombole Naomi, kuti amutenge Rute. Mwaona? O, ndi chithunzi chokongola bwanji! Ndiuzeni ine kuti Mawu a Mulungu ndi osadzozedwa? [M'bale Branham akusonya Baibulo lake—Mkonzi.] Chidutswa chirichonse cha Ilo, chikuyankhula za Kudza!

Ndipo Rute, tsopano kudikirira.

143 Ndipo Boazi, mfumu ya kukolola, kapena mbuye wa kukolola, akupita kunja kwa zipata, ndipo akuwaitana akuluakulu onse amu mzinda; ndipo anapanga umboni wapagulu, kunja kwa chipata. Iye anati, “Onani kwa izo, anthu nonse inu!” Iye anavula nsapato zake, anaziponya izo pamaso pa iwo, ngati umboni. Anati, “Ine, tsiku lino, ndawombola chuma chonse chotaika cha Naomi. Ndipo katundu wake yense ndi wanga, tsiku lino.” O, mai!

144 Konzekani, ndi izi apa. O, ine ndikungomverera chinachake chikusuntha. Zindikirani, Khristu, pamaso pa akuluakulu a Israeli, anawatsogolera kunja kwa zipata za mzinda, ndipo anakapanga umboni. “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu; ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Umboni wa pagulu, Iye wauwombola Mpingo kuchokera (ku chiani?) chikhalidwe chake chotaika. Mmunda wa Edeni, ife tinalibe kudwala kulikonse; mmunda wa Edeni, ife tinalibe tchimo; mmunda wa Edeni, ife tinalibe imfa. “Ndipo Mulungu analikonda kwambiri dziko lapansi, Iye anapereka Mwana Wake wobadwa yekha,” anakapanga umboni kunja kwa chipata, kuti Iye anali atakonza njira yothawirapo kwa onse omwe ankafuna kuti abwere. Ndi chithunzi chokongola bwanji! Ine ndikuyembekeza inu mukukhoza kuziwona izi. Tsopano Ambuye adalitsidwe!

Ndipo momwe ine ndikuwonera, mwinamwake, nthawi yanga ikutha.

¹⁴⁵ Mulungu akupanga njira yoperekedweratu, ndipo Iye anaipanga iyo mwa Yesu Khristu. Pamene Yesu anapita uko ku phiri la Gologota, anavulazidwa, akuukha magazi, mtanda kukhukhuluzika moponda mapazi amagazi pamene Iye anali kukwera phiri. Anapita pamwamba apo; umboni wa pagulu, “Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu; ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Atafa, anakwera Mmwamba. Inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndipo anatomiza kuno mphatso zauzimu kwa Mpingo, kupanga njira yoperekedweratu. Ndipo chisangalalo ichi chomwe ife tiri nacho mu mitima yathu tsopano, ndi kulipira kwapang’ono kokha, ndalama zachikole, pa zomwe ziti zidzakhale pamene ife tidzaombedwa kwathunthu. Ndipo machiritso Auzimu awa omwe ife tiri nawo tsopano ndi chikole cha chiombolo chathu cha thupi lathu. Ife ndife owombedwa. Mulungu anapanga Nsembe yoperekedwa.

¹⁴⁶ Ine ndiyenera kuti ndiime, abwenzi, chifukwa anthu akudzuka ndi kumatuluka.

¹⁴⁷ Ine ndimanena kwa mkazi wanga, tsiku lina, “Ine ndalalikira mu pafupi, ine sindikudziwa ndi mafuko osiyana angati, mu mzinda uliwonse kudutsa mu United States yense. Ndipo Louisville, Kentucky ndi malo okha omwe anthu anayamba anyamuka namatuluka pamene ine ndinali kulalikira.” Ndi kulondola, kwathu, onani, malo okha omwe ine ndinayamba ndawawonapo.

¹⁴⁸ Ngati aliyense wazizindikira izo, yemwe anakhalapo mu misonkhano ina ndi ine, kwezani mmwamba manja anu, mchipinda monse. Ndithudi.

¹⁴⁹ Kuzungulira, kwina kulikonse, ndipo sindinayambe ndakhalapo nazo izo kulikonse mu moyo wanga koma kuno ku malo akwathu komwe, Louisville, Kentucky. Anthu amadzuka ndi kumapita kunja, pamene iwe ukuyamba kuti uwuyale Uthenga bwino kwa mzere wodulizira. Iwo amachita izo. Ndipo ine sindinayambe ndakhalapo nazo izo kwina kulikonseko, kulikonse mu dziko, kumene ine ndinayamba ndakhalako; ngakhale ku Afrika, malo ena onse, Sweden, Norway, kumene kumakhala mateni a masauzande. Mwa ganizo langa lodzichepetsa, ine sindinayambe nthawi imodzi ndachitirapo umboni munthu mmodzi akuchoka, kudzuka ndi kumatuluka, pamene ndikulalikira; komwe kuno kokha.

¹⁵⁰ Inu mukuona, abwenzi, sabata ino ine ndalimbana nazo molimba kuti ndiyesere kuwatsimikizira anthu ena, kuti . . .

¹⁵¹ Mawu a Yesu Khristu, ziribe kanthu chomwe Iwo ali, ayenera kukhala olondola. Iye anati, “Mneneri samakhala wolemekezeka pakati pa anthu ake omwe, dziko lakwawo lomwe.” Ndipo uko nkulondola ndendende. Iwo sangawalandire basi Iwo. Ine sindikudziwa chifukwa chake. Yesu ananena chomwecho, ndipo

izo zikukhazikitsa icho. Ine ndiri nawo anthu kuzungulira dziko lino, omwe akanati alolere pafupi kuti andifere ine. Iwo amandikonda ine. Koma mwa kugwira kwawamba, ndi Mawu a Mulungu; ndipo Mulungu ayenera kumasunga Mawu Ake, polinga kuti akhale Mulungu. Ndiko kulondola.

¹⁵² Ndipo aliyense yemwe anakhalapo mu misonkhano kale, kunja kwa kuno, ife takhalapo nazo zizindikiro ndi zozizwitsa zochepetsetsa zomwe zinachitidwapo mu msonkhano uliwonse umene ine ndinayamba ndawuwonapo wa—wa utali chomwechi. Kawirikawiri pamakhala akhungu, ogontha, osayankhula, olumala ndi chirichonse, zikuku zitaunjikidwa pa ngodya, ndi anthu akupita mmalo, ndi timabedi ndi machira.

¹⁵³ Ndipo alipo kokha, monga momwe ine ndikudziwira, pali anthu awiri ali muno. Ine ndinamuwona mmodzi wa iwo, poyamba, mnyamata uyu pano, ali apoyo. Ndinawona Mzimu Woyera utaima pa iye usiku wina, unabwera pafupi kwambiri. . . Ine ndikanakhoza kulengeza machiritso ake, ndipo basi pamene ine. . . ine ndisanathe kulalikira; koma ine ndinawuona Iwo ukugwera mmbuyo kutali ndi iye, unayamba. . . Chinachake chinadutsa pamalo ake apo, ndipo chinalepheretsa Iwo kwa iye. Ndi munthu yekha ndinamuwona ngakhale wosautsidwa mwa njira iliyonse, kunja kwa anthu angapo ogontha, kapena chinachake anadza ku nsanja, iwo anandiuza ine za izo. Ine sindikudziwa. Koma ndi inu apo. Ndi kwathu. Ndi cha kwa abale ako.

¹⁵⁴ Tsopano, kwa mzanga wabwino, Bambo McSpaddin, Bambo McDowell, ndi iwo omwe ali mchipindamu, usikuuno, omwe ine ndayesera kuti ndiwauzeke izi. Ndi inu anthu aku Jeffersonville, ochokera ku kachisi, kodi inu mukuona zomwe ine ndimazikamba? Inu simungakhoze kuwasintha Mawu a Mulungu. Iwo adzakhala kwa nthawizonse mwanjira imeneyo, chifukwa Yesu ananena chomwecho.

¹⁵⁵ Tsopano, ndipo kwa anthu omwe amandipempha ine kuti ndibwerere ku kachisi, kodi inu mukuona chifukwa chake? Komwe mwinamwake kukhala anthu fifite atapulumutsidwe sabata ino, cha kuno, mu chitsitsimutso; mwinamwake osati ochuluka chomwecho, mwinamwake osati teni, pa zonse zomwe ine ndikuzidziwa. Komwe, mwawamba, mu masiku eyiti, iwo akanachulukira mu mahandiredi ndi mahandiredi ndi mahandiredi, kwina kwake. Mwaona? Mukuona kusiyana kwake? Ndi kwathu. Ndi pakati pa abale ako.

¹⁵⁶ Osati chifukwa iwo samandikonda ine, koma chifukwa Yesu ananena chomwecho. “Ndipo pamene Iye anapita kwa abale Ake Omwe, chinthu chokha chomwe Iye akanakhoza kuchita chinali kusanjika manja pa anthu odwala apang’ono ndi kuwachiza iwo; kunalibe ntchito zamphamvu zomwe Iye akanakhoza kuzichita.” Ndi kulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndi

kubwereza Lemba uko. Ndipo umo ndi momwe izo zimayenera kukhalira. Ndiko kulondola. Si ineyo, pambuyo pa zonsezi. Ndi Iyeyo. Ndi Iyeyo basi. Ngati ine ndikadakhala mchiritsi . . .

¹⁵⁷ Ine ndiri naye m'bale yemwe ali mchipatala, usikuuno, yemwe Mulungu anandisonyeza ine, chaka chapitacho. Ndipo ine ndikulingalira ziripo mboni thuu handiredi pano pomwe, za mnyamata wabwino ndi wathanzi. Koma Mulungu anatomiza masomphenya ndipo anati, "Iye akupita." Ndipo ziribe kanthu chomwe chiti chichitike, iye akupita.

¹⁵⁸ Adotolo anati, osati kale litali, "Ife tikhoza kumupulumutsa iye." Koma iwo sanatero, ndipo iwo sakhoza.

¹⁵⁹ Ine ndinawuona Mzimu Woyera ukudza, kudzasonyeza masomphenya, ndi kulemba manda ake, ndi kuti, "Iye ndi wotsatira wake." Ndipo ndi momwe izo ziti zidzakhalire. Ndi angati anandimva ine ndikunena izo, kale, kale, kale litali? Kwezani manja anu. Ndiko kulondola, pamene mnyamatayo anali wamkulu, wojintcha, ndi wathanzi. Iye ayenera basi kuti azipita. Ndizo zonse. Motani? Ngati ine ndikanakhala mchiritsi, ine ndikadamuchiritsa iye. Uyo ndi wanga yemwe, m'bale wanga yemwe.

¹⁶⁰ Koma pamene Mulungu anena, Mulungu asunga Mawu Ake. Ndipo ndicho chifukwa ine ndimadziwa chomwe ali, PAKUTI ATERO AMBUYE. Ine ndidzafa ndi Ichu, pakuti Iwo ndi Mawu a Mulungu ndipo Iye aziwasunga Iwo. Iye wapereka Njira, ndipo ndine wokondwa kuilandira Iyo usikuuno, Ambuye Yesu Khristu. Si choncho inu? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Mulole madalitso Ake Amuyaya akhale pa inu.

¹⁶¹ Ndipo kachiwiri ine ndikuti, Nsembe yoperekedwa ya Mulungu, usikuuno, njira yothawirapo, ndiyo kupyolera mwa Yesu Khristu. [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] Pamene, Yesu Khristu anapereka mpingo kwa osakhulupirira, kuti iwo azikhoza kulowamo ndi kuwona mawonetseredwe a chiukitsiro Chake, ndi kudziwa kupyola mthunzi wa kukaikira kuti Iye anauka kwa akufa. Yesu anauka kwa akufa, kupanga njira yoperekedweratu, kwa yense yemwe afuna azikhoza kuyang'ana ndi kukhala moyo. Koma ngati inu mukana kuyang'ana, inu mungakhoze bwanji kuchita china chirichonse kupatula kufa? Yesu anati, "Ngati inu simukhulupirira kuti Ine ndine Iye, inu mudzafa mu tchimo lanu." Izo nzoona.

¹⁶² Abwenzi, ine nthawizonse ndayesera kusunga kukhazikika kwa pa msewu. Iwe ukatengeka ndi zamaonekedwe, mwa maonekedwe basi ndi a mipingu monga iwo angakhoze kukhalira, anthu amagwira ku gawo ilo. Ndiye ngati iwe susamalira, iwe umafika powulukira ku tsidya lina, ndi kungokhala wotentheka basi monga iwe ungakhalire. Koma pali pakati pa msewu, pamene Uthenga wooka, womveka, woganizabwino umalalikidwa, ndipo Mulungu amayenda

pamenepo, akutsimikizira Choonadi. “Khwalala ndilo chipata, ndipo njirayo ndi yopapatiza, koma adzakhalapo ochepa ati adzaipeze Iyo.” Chabwino.

¹⁶³ Kwa inu gulu laling’ono la anthu kuno usikuuno, mwakhala muno, mulole chikondi cha Mulungu chikufungatireni inu usikuuno. Ndipo makamaka odwala, osowa, ine ndikupemphera kuti pasakhale mmodzi wa inu koma yemwe ati apite kwawo wochiritsidwa. Ngati ine ndikanakhoza kuchitapo kalikonse pa izo, ine ndikanachita izo mokondwera; koma ine sindingakhoze kuzichita izo. Chinthu chokha chimene ine ndingakhoze kuchita ndi kumuimira Iye kwa inu, mwa njira ya mphatso Yauzimu.

¹⁶⁴ Tsopano ngati ine ndikunena Choonadi, kuti Mulungu anapereka nsembe; ndipo Nsembe imeneyo, Yehova-Yire, inali Yesu Khristu. Ndipo maina onse seveni apawiri, achiwombolo anali mwa Yesu Khristu. *Yehova-yire*, “nsembe yoperekedwa ya Ambuye.” *Yehova-rafa*, “Ambuye yemwe amachiza matenda anu.” Ndi *Yehova*-. . . “mbendera.” N—ndi ena onsewo, maina apawiri seveni, onsewo anali mwa Khristu Yesu. Ndipo apo ndi pamene zoimira zonse ndi mithunzi, ya Chipangano Chakale, zonse zinadza ndipo zinadzakomana mwa Yesu Khristu. Iye analipira mtengo wapamwamba, anakwera Mmwamba, ndipo wautumizanso Mzimu Woyera, usikuuno, yomwe ili njira yoperekedwa ndi Mulungu ya pothawirapo panu.

¹⁶⁵ [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.] . . . ife tikanakhala nayo nthawi kuti tipite mu izo.

¹⁶⁶ Ine ndikukhoza kuwawona anzeru akupachira ngamila zawo, mwamsanga ndithu. “Inu mukupita kuti, okonedwa?” akutero akazi awo.

¹⁶⁷ “Ine ndikupita kukaiwona Mfumu yaing’ono yomwe yabadwira, kutali ku Palestina.”

“Chabwino, inu simunatenge ngakhale namlondola wanu.” Iye anati, “Ine sindikusowa namlondola aliyense?”

¹⁶⁸ “Inu mukadutsa bwanji mu zipululu, ndi mzigwa, ndi mmapiri, opanda namlondola?”

¹⁶⁹ Iye analoza mmwamba kwa Nyenyezi, anati, “Ine ndikupita mwa njira yoperekedwa ndi Mulungu.” Nyenyezi inamutsogolera iye molunjika ndithu kwa Yesu.

¹⁷⁰ Ndipo mvetserani, ife tisanatseke. Mulungu ali nayo njira yoperekedweratu pano usikuuno; osati kupyolera mu mpingo, osati kupyolera mu zamulungu. Koma kupyolera mu Mzimu Woyera, udzakutsogolerani inu ku njira yoperekedwa ndi Mulungu ya kuyeretsedwa kwanu, kuchiritsidwa kwa thupi lanu, ubatizo wa Mzimu Woyera, chisangalalo, chimwemwe, mtendere, ndi chirichonse chomwe inu mukuchisowa. Yesu Khristu ndi nsembe yoperekedwa ndi Mulungu.

171 Ndipo ine ndikunena kuti Iye anauka kwa akufa, anakwera Mmwamba, anautumiza mmbuyo Mzimu Woyera ngati njira yoperekedwa ndi Mulungu kuti uziwutsogolera Mpingo. Iye anati, “Iye sadzayankhula za Iyeyekha, koma Iye adzachitira umboni za Ine,” Yesu anatero. “Ndipo pamene Iye adza, Iye adzabweretsa zinthu izi ku kukumbukira kwanu, ndipo adzakusonyezani inu zinthu ziri nkudza. Pakuti zinthu zomwe Ine ndikuchita inunso muzidzazichita. Dziko silidzaziwona izo, koma inu muzidzaziwona izo. Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mkati mwanu, mpaka kumapeto a m’badwo.”

172 Imva izi, Louisville, Uthenga wanga wotsiriza kwa iwe! Nsembe yoperekedwa ndi Mulungu ndi Yesu Khristu, Mmodzi woukitsidwayo pano akuupatsa mphamvu Mpingo mwa Mzimu Woyera. Uku ndiko Kuwala. Muziyenda inuyo mu Iko, mupeza mpumulo kwa solo yanu, kuchiritsa kwa matenda anu.

Tiyeni ife tipemphere.

173 Atate Akumwamba, O Mulungu, pamene tsiku...Pansi pomwe mwakuya mu solo yanga, ine ndikudabwa, monga ine ndapangitsidwa kuti ndidabwe, powona fuko lalikulu lokongola ili la Amereka, ndi kuwaona mabomba aakulu awo kunja uko akuyikidwa kudutsa nyanja. Anthu authakati, opanda umulungu omukana Mulungu, omukana Ambuye Yesu Khristu, Mzimu Woyera, ndi uthakati wonse ndi kupulupuza, ndi machenjerero omwe Satana angakhoze kuwakankhira mu malingaliro awo kuti aliwononge dziko lino, kuchita ndendende basi monga Inu munati ilo likanadzachita, “kuliwotcha ilo ndi kutentha.” Ndipo ngakhale asayansi aakulu a mdziko akuti, “Mkati mwa zaka teni padzakhala kutheratu kwa psyiti, palibe mmodzi adzasiyidwe, palibe chidzakhale moyo pa dziko lapansi; litasesedwa konse ndi bomba la haidrojini.”

174 O Mulungu, amuna ndi akazi ali pano, osakonzeka usikuuno. Inu mwakhala, sabata ino, waulemerero kwa ife. Ife takhala mu malo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu, ndipo ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha oyer okonedwa awa mu Louisville. Mulungu, mulole iwo apite kuchokera ku msonkhano uno, ndi liwu la chenjezo, konse kozungulira.

175 Wokonedwa Atate Akumwamba, ine ndikupemphera kuti Inu mumutumize wina muno ndi chitsitsimutso cha kachitidwe-kachikale, chomwe chiti chigumulire pansu makoma ozungulira Louisville. O, chitani, Mulungu. Mulole okonedwa ambiri abweretsedwe ku chidziwitso chopulumutsa cha Ambuye wathu Yesu Khristu.

176 Ine ndachita mwakupambana kwanga, Ambuye Yesu, zonse zomwe ine ndikuzidziwa kachitidwe kake, kupereka liwu motsutsa tchimo zolimba momwe ine ndikudziwira, ndipo Inu mwakhala ochuluka mwaulemerero kwa ife. Inu mwatsimikizira Mawu aliwonse ndi zizindikiro ndi zodabwitsa.

Ife tikukuthokozani Inu. Tsopano, Atate, kwa zotsatira, ife tikuzisiya izo zonse kwa Inu. Mulole chifuniro Chanu kuti chichitidwe.

¹⁷⁷ Mudalitseni M'bale Cauble, Ambuye, m'bale wathu. Mudalitse antchito ake onse, ndi azitumiki ena onse. Ife tikuganiza za M'bale Durban wamng'ono, kumusi kuno, ndi abale ena awa kuzungulira kuno, omwe ali abale abwino; akuyesera mwakukhoza kwawo kuti akhomerere motsutsa tchimo ndi uthakati, kachasu ndi kumwa, ndi kupitiriza, ndi kusonkhanira, kapena chirichonse mozungulira mzindawu. Iwo akuyesera kuti apereke liwu la chenjezo. Mulungu, adalitseni amuna awo ndi kuwadzoza iwo ndi Mzimu Woyera. Perekani izo, Ambuye. Mulole iwo akhale antchito abwino, ali nako kupambana kwakukulu kwa kuwaitana anthu kuchokera mu mdima, kupita mu kuwala kopambanaku.

¹⁷⁸ Ndipo tsopano, Ambuye, mu msonkhano wotsekera, usikuuno, kodi Inu simubwera? Ingobwerani kamodzinso, Mzimu Woyera waukulu, Mphamvu Yaumulungu, ndipo tifungatireni ife ndi dalitso Lanu. Ndipo mulole Mngelo wa Mulungu aime pa nsanja pano, ngati mboni ya chiukitsiro cha Nsembe yoperekedwa ndi Mulungu, Ambuye Yesu Khristu. Ndipo mulole Iye achite zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa, mu kutsimikizira kwa Mawu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina Lake, Mwana Wanu wokonedwa, Yesu Khristu. Amenii.

¹⁷⁹ Ambuye atakudalitsa iwe, mzanga Wachikhristu. Tsopano ine ndikufuna kuti ndiwapempherere odwala. Ine ndikufuna kuti ndikufunseni inu tsopano, isanafike nthawiyo. Kodi alipo munthu mmodzi alipo mu nyumba muno, yemwe sanapulumsidwe, sanatero panobe, ngakhale kuchuluka kotu atembenezidwe, akumupempha Khristu kuti akhululukire machimo awo? Ine ndikukufunsani inu mwapoyera, mwanjira yolimba basi. Ndipo ine ndikukhulupirira kuti inu mukhala mwamuna kapena mkazi mokwanira, kapena mnyamata kapena msungwana, kuti muchita izo. Ngati inu simunayambe mwamulandirapo Yesu ngati Mpulumutsi wanu, ndipo mukufuna kuti muchite izo tsopano, kodi inu mungaime pa mapazi anu ngati wokhulupirira, ndi kuti, "Ine tsopano, kuyambira ora lino, ndikhala wokhulupirira mwa Yesu Khristu." Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, dona.

¹⁸⁰ Inu mukuvomereza chikhulupiriro chanu mwa Yesu Khristu, pamene inu mukuchita izi. Pafupi miyoyo isanu, ikanafa maminiti asanu apitawo, ikanabwerera mmbuyo ku Muyaya wamdima. Ngati iwo angafe tsopano, iwo aphimbidwa ndi Magazi.

181 Wina woonjezera, alikuti iye? Kumbuyo komwe, Mulungu akudalitseni inu. Inde, m'bale wanga. Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Uyo, Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Uko nkulondola. Basi mwachikale molimba... Mulungu akudalitseni inu, m'bale, mukumuvomereza Yesu. Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Mulungu akudalitseni inu. Uko mkhonde, kwinakwake? Mulungu akudalitseni inu, mlongo.

182 Izo ndi zodabwitsa. O, mai! Ine ndikukhumba ife tikadakhala nao malo ena pano a mpando wa olira akachitidwe-kachikale ndi kuitanira kuguwa. Ndi zomwe ife tikuzisowa pakali pano.

183 Ndi angati mkati muno akuti, "M'bale Branham, ine ndakhala ndiri wochimwa, koma tsopano ine ndikuvomereza, ndikumulandira mu mtima mwanga, Yesu Khristu, nsembe yoperekedwa ndi Mulungu"? Pafupi madazeni awiri aima. Kodi inu mungaime ndi kuti... Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, mnyamata. Ndizo zabwino. Mulungu akudalitseni inu. Winawakenso aime, ndi kuti, "Tsopano ine ndikumulandira Yesu Khristu pakali pano, ngati Mpulumutsi wanga. Ine ndikupanga kuvomereza uku mwapoyera, pamaso pa anthu ndi pamaso pa Mulungu, kuti ine tsopano ndikulandira machiritso a Mulungu kwa tchimo langa, Yesu Khristu." Kodi pangakhale mmodzi winanso, cha kuno, paliponse? Mulungu akudalitse iwe, mnyamata. Ndiko kulimbantima. Mulungu akudalitseni inu. Ndizo zabwino.

184 Wina wakenso angaime, ndi kuti, "Ine tsopano ndikumulandira Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wanga wanga, ine ndikutengera nsembe yoperekedwa ndi Mulungu kwa tchimo langa"? Mulungu akudalitseni inu, abambo; bambo wokalambirapo, mutu-waimvi, akunjenjemera, akuima kuti amulandire Yesu Khristu ngati Mpulumutsi.

185 Tsopano, Mulungu akuudziwa mtima wanu; Iye akuyang'ana kumene pa inu. Mulungu akudalitse iwe, mnyamata. Ine ndinakuwona iwe apo, wavala juzi yofiira, ukuimirira. Chabwino, wina wakenso, imirirani ndi kuti, "ine ndikuvomereza." Mulungu akudalitseni inu, ndi inu, dona ndi mnyamata wamng'ono mmwamba apo. Mulungu akudalitseni inu. Mulole Mulungu...

186 Dzina lanu likupita pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa pamene inu mukuima mwapagulu pamaso pa omvetsera awa. "Iye amene andivomereza Ine pamaso pa anthu, iyeyo ine ndidzamuvo mereza pamaso pa Atate Anga ndi Angelo oyer. Ngati inu mukuchita manyazi ndi Ine kuno pamaso pa anthu, Ine ndidzachita nanu manyazi inu pa Tsiku limenelo."

187 Kodi inu mwakhala ochimwa kwambiri, ndipo mukufuna kuti mukhululukidwe? Munthu wina aliyense yemwe sanaime

panobe, ndipo akufuna kuti aime, basi kuti ayilandire nsembe yoperekedwa ndi Mulungu ya tchimo lanu, kodi inu mungaime? Wina... Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Uyo ndi mnyamata wachisilikari. Mulungu akudalitse iwe cha kuno, aponso. Ambuye akhale ndi iwe, m'bale wanga.

¹⁸⁸ Kodi angatero wina wakenso? Chabwino. Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Ndizo zabwino. Winawakenso akufuna Moyo Wamuyaya, pa kumuvomereza Yesu Khristu? Mulungu akudalitseni inu. Inde. Mulungu akudalitseni inu, atatu inu, uko mu khonde lammwamba.

Kodi si zodabwitsa izo? Ena sate, kapena kupitirira, tsopano. Chabwino.

¹⁸⁹ Mulungu akudalitseni inu. Ndiyo njira yake, yomuvomerezera Yesu, Nsembe yoperekedwa ndi Mulungu. Iye ndi ndi Yehova-Yire. Chabwino. Ambuye akudalitseni inu mu khonde lammwamba, mlongo wanga, akupatseni inu Moyo Wamuyaya.

¹⁹⁰ Tsopano inu mukupeza kukonedwa ndi Mulungu. Mulibe Mkristu mkati muno, yemwe amadziwa kalikonse za Mulungu, koma akudziwa kuti maminiti otsiriza faifi'wa, chikhalidwe chasintha, kwathunthu, mu nyumba muno. Ndiko kulondola. Mwaona? Basi mu mphindi ya mdima, ndiye Yesu amabwerapo.

¹⁹¹ Winawake akuti, "Ine tsopano ndikumuvomereza Yesu Khristu. Ine..." Mulungu akudalitseni inu, dona. "Ine ndikumuvomereza Iye, ndikufuna kuti dzina langa lilembedwe pa Bukhu Lake. Ine ndikumuvomereza Iye pakali pano ngati wolamulira wanga wamkulu wa moyo wanga." Mulungu akudalitseni inu, bwana. Mulungu akudalitseni inu.

¹⁹² Wina wakenso, wobwerera mmbuyo, mungaime ndi kuti, "Ine nthawiyina ndinali Mkristu, M'bale Branham, koma ine ndapita kutali, nkuchoka kwa Mulungu. Usikuuno, ine ndikubwera Kwathu"? Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Mulungu akudalitseni inu, m'bale. O, Mulungu akukuwonani inu. Mulungu akudalitseni inu, dona. Mulungu akudalitseni inu, m'bale. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Ndiko kulondola. O, mai! Mulungu akudalitseni inu, m'bale; ine ndikukuonani inu m'khonde lammwamba. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, m'bale ali ndi manja ake mmwamba. Wina wakenso? Mulungu akudalitseni inu, dona. Ndizo zodabwitsa. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Ndizo zodabwitsa. Ndizo... Pitirirani kumangobwera. Ndipo Mulungu akudalitseni inu, mlongo; ine ndikukuonani inu mukuima. Mulungu akudalitseni inu, bwana, pamwamba apo pa nsanja, muli ndi dzanja lanu mmwamba. Mulungu akudalitseni inu.

193 Mmbuyo, komwe mmbuyo, winawake angati, “M’bale Branham, ine tsopano ndabwerera mmbuyo; ine ndikubwera Kwathu. Ine ndikuvomereza kukonzedwa kwanga, Yesu Khristu, nsembe yoperekedwera ku kubwerera mmbuyo kwanga. Ine ndikubwera Kwathu, usikuuno womwe. Ine ndikuzikonza izo pakali pano, tsopano ndi kwanthawizonse. Ndipo ine ndikudziwa kuti pamene...”? [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

Tsegulani mikono Yanu ya chikondi,
Ambuye, ndikudza Kwathu.

Ndikudza Kwathu, ndikudza Kwathu,
Kosalowereranso;
Tsegulani mikono Yanu ya chikondi,
Ambuye, ndikudza Kwathu.

194 Ndikudabwa ngati ife tingati tiing’ung’uze iyo. [M’bale Branham akuyamba kung’ung’uza *Ambuye, Ine Ndikubwera Kwathu*—Mkonzi.]

195 Pamene iwo akuing’ung’uza iyo, kodi alipo mmodzi muno, wasiyidwa, angati, “Ambuye, Inu mukundiwona ine pamene ine ndaima. Ine ndikubwera Kwathu tsopano. Ine ndatopa nako kulowerera uku, mtendere wosakhazikika. Ine ndikuivomera njira yanu yotulukiramo, Yesu Khristu ngati Mpulumutsi wanga. Ine tsopano ndikubwera, Ambuye, basi momwe ine ndiriri. Ine ndikubwera; kukweza mmwamba dzanja langa. Ine ndikuti ndiyime ndi kukulolani Inu muwone, ndi omvetsera awa, kuti ine tsopano ndikukhulupirira, ndipo ine ndikubwera Kwathu”? [M’bale Branham akung’ung’uza *Ambuye, Ine Ndikubwera Kwathu*.] Mulungu akudalitseni inu, mlongo.

Ndikudza Kwathu, ndikudza Kwathu, wo- . . .

196 Yense yemwe akumverera mu mtima mwawo kuti iwo akufuna kuti amuvomereze Iye, ingoimani pa mapazi anu.

Tsegulani mikono Yanu ya chikondi,
Ambuye, ndikudza Kwathu.

Muzingopitirira nayo, ngati inu mukufuna, mlongo.

197 Ine ndikuti ndikufunsi inu chinachake tsopano. Munthu aliyense yemwe anaima, ine ndikufuna kuti inu muime pa mapazi anu pamene ine ndikuperekerera pemphero kwa inu. Munthu aliyense yemwe anaimirira, aime kachiwiri, kwa mphindi pang’ono zokha. Ingoimani, paliponse mchipinda. Aliyense yemwe anaima, aime kachiwiri, paliponse, mmakonde ndi paliponse, kuti ife tikhoze kupereka pemphero. Ndi choncho. Ndi choncho. Wina aliyense wa inu yemwe anaima, yemwe anaima kanthawi kapitako. Ndipo ngati alipo enanso omwe akufuna kuti aime ndi iwo, pomuvomereza Khristu, kodi inu muima tsopano. Mulungu akudalitseni inu.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano.

198 Atate Akumwamba achifundo, awa tsopano akubwera ngati ana Anu. Iwo abwera kale. Mphindi yomwe Mzimu Woyera unayankhula kwa solo yawo, iwo anaimirira ndipo anakulandirani Inu, ndipo Inu munawapatsa iwo Moyo wosatha. Mulungu, adalitseni iwo. Yenda nawoni iwo kupyola mmoyo, Atate. Ena a iwo akhala ali antchito Anu, nthawi zapitazo, koma anagwera kwina; ndipo, usikuuno, Mzimu Woyera, mwa kulalikira kwa Mawu, unabwera pansi ndipo unawadzoza iwo. Ndipo iwo tsopano aima, kukuvomerani Inu, ndi kukupatsani Inu mathokozo chifukwa cha Moyo wawo Wamuyaya womwe iwo ali nawo tsopano mwa Yesu Khristu. Zikomo Inu, Atate. Mulole moyo wawo ukhale wokondwa ndi wosangalatsa. Mulole matenda akhale kutali ndi chitseko chawo. Ndipo mulole iwo akhale miyoyo yaitali, yokondwa; ndipo afike pa mtendere, kulowa mu Ufumu wa Mulungu, pa mapeto a dziko. Mu Dzina la Yesu Khristu ife tikupempha izi. Amen.

199 Mulungu akudalitseni inu. Ndipo anthu anati... [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Amen. Mulungu akudalitseni aliyense. Ngati inu mwakhala pafupi ndi winawake yemwe anaimirira; mugwirane chanza nawo, Mkhristu, ndipo muwauze iwo kuti ndinu wokondwa chifukwa cha iwo.

200 Ife tiribe malo kuno, kuti tiwaitanire iwo pozungulira guwa. Ife tiribe basi—malo kuno kuti tichite izo. Ambuye akudalitseni inu; yochuluka, miyoyo yochuluka.

201 Tsopano inu mukudziwa, molingana ndi Mawu a Mulungu, chimene chikuchitika Kumwamba pa nthawi ino? Angelo akusangalala. Mbendera zakuda za Satana zagonjetsedwa; izo ziri pansi ndipo athamangitsidwa. Ndipo Angelo ndi mbendera zawo zoyera za chigonjetso zikuuluka Kumwamba konseko usikuuno, ndipo mabelu a Ulemerero akuimba, akungoimba nthetemya, pamene wochimwa mmodzi akudza kwa Khristu. Ambuye adalitsidwe ndi kutamandidwa kwanthawizonse! O, mai!

202 Ine ndikungokhulupirira ife tikhala ndi msonkhano wa machiritso weniweni tsopano. Inde? Chiani? Makadi apemphero? [Malo osajambulidwa pa tepi—Mkonzi.]

203 Ine, pa utumiki uwu, ndikutenga mzimu uliwonse, mu chipindachi, pansi pa ulamuliro wanga, kwa ulemerero wa Mulungu. Chifukwa chomwe ine ndikunenera izo, izo zikuika Dzina la Yesu Khristu pamwamba pa omvetsera onse. Ngati Satana ati azichita mwamwano, inu muwona zomwe ziti zichitike. Iwo mwinamwake akhoza kuwanyamula iwo kuwatulutsa pa khomo, atachoka mu dziko lino, mwaona.

204 Tsopano, kotero inu muyenera mukhale omvera. Musati muimirire ndi kumayendayenda. Mukhale bata. Matenda awa amapita kuchokera kwa wina kupita kwa wina. Inu mukudziwa, masikolala a Baibulo, kuti izo ndi zoon.

Mwaona? Osati kusewera zampingo tsopano. Ndipo ine ndiribe choyankhira kwa otsutsa kapena osakhulupirira. Imvani izo! Ine ndikuyankhula mu Dzina Lake.

²⁰⁵ Tsopano, Mngelo wa Ambuye, pafupi, ine ndikudalira kuti Mulungu awonetsera chiukitsiro cha Mwana Wake.

²⁰⁶ Tsopano inu mubwere pafupi. Ine ndikulingalira, mlongo, inu ndi ine taima pano limodzi, kuti ndife alendo kwa wina ndi mzake. Ine sindikukudziwani inu. Ine sindinayambe ndakuwonanipo inu. Koma Mulungu akutidziwa tonse ife. Ndinu munthu chabe yemwe munabweretsedwa kuchokera mwa omvetsera. Ena a iwo anakupatsani inu khadi la pemphero, linali ndi nambala pa ilo. Inu munangoitenga nambala yanu, ndipo iyo inaitanidwa, ndipo ndi inu pano.

²⁰⁷ Ndipo inu simukusowa kuti mukhale ndi khadi la pemphero. Aliyense yemwe ali mwa omvetsera, ingoyambani kupemphera; muwone ngati Mzimu Woyera suli chimodzimodzi usikuuno, umene uli pa mpingo, umene unali pa Yesu Khristu. Muwone ngati Iwo suli. Ngati Iwo suli, ngati Iwo suli, ndiye ine ndaimira molakwika Uthengawu kwa inu, ndiye ine ndikhala mboni yabodza ya chiukitsiro. Ngati Mulungu ati atsimikizire izi kuti ndi Choonadi, ndiye ine ndakuuzani Choonadi, ndipo Mulungu wanena kuti ndi Choonadi.

²⁰⁸ Tsopano, dona pano, mlendo, sindinayambe ndamuwonapo iye mu moyo wanga. Iye sanayambe wandiwonapo ine, ine ndikulingalira. Iye tangokomana pano, ndizo zonse. Ine sindikumudziwa iye. Mulungu akumudziwa iye.

²⁰⁹ Tsopano, pamene Ambuye wathu Yesu anali kuno, Iye anayankhula kwa mkazi nthawiyina, Iye anali asanamuwonapo konse mu moyo Wake. Iye anali akutungako madzi pa chitsime. Ndipo Iye anati, “Ndi bweretsere Ine akumwa.” Ndipo Iye analankhula naye iye utali wokwanira kuti augwire mzimu wake, ndiye Iye anamuza iye pamene vuto lake linali.

Ndipo iye anati, “Chabwino, ine ndikuzindikira kuti Ndinu mneneri.”

²¹⁰ Tsopano, Yesu anati, “Zinthu zimene Ine ndikuzichita inunso muzidzazichita, mpaka kumathero a dziko.”

²¹¹ Mwamuna anabwera mu mzere Wake wa pemphero, nthawi yina; iye anali mwamuna wolungama. Iye anati, “Iwe ndiwe Mkhristu, munthu wabwino, munthu wolemekezeka.”

²¹² Iye anati, “Ndi liti pamene Inu munandidziwa ine, Rabbi?” Kapena, “Abusa, Mphunzitsi,” chirichonse chimene inu mungatanthauzire apo.

²¹³ Iye anati, “Filipo asanakuitane iwe, pamene iwe unali pansu pa mtengo, ine ndinakuwona iwe.” Mwa kuyankhula kwina, “Iwe umapemphera usanabwere ku msonkhano, ndipo Ine ndinakuwona iwe ukuchita izo.”

214 Iye anati, “Inu ndinu Mwana wa Mulungu. Ndinu Mfumu ya Israeli.”

215 Tsopano ngati Yesu wauka kwa akufa, ndiye Iye achita izo mofanana.

216 Tsopano, omvetsera, tsopano Iye ali pano, Mngelo wa Ambuye. [Mlongo ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Inu mukuzindikira za izo tsopano, kuti chinachake chinachitika apo pomwe. [M’bale ati, “Ameni.”—Mkonzi] Si zoona izo? [“Ameni.”] Ndi zoona. Iwo uli pano?

217 Tsopano, kukuchizani inu, ine sindikanakhoza. Moyo wanu inu simungakhoze kuwubisa, pakuti inu simuli mu kukhalapo kwa m’bale wanu; ndi mu Kukhalapo kwa Iye. Kodi icho si choonadi? Ndipo inu mumukhulupirire Iye ndi mtima wanu wonse, kuti Mulungu watitumiza ife kuno kuti tidzayese kukuthandizani inu. Pambali pa kukhala wodwala, inueni, inu muli naye wokonedwa yemwe akudwala. [Mlongo ati, “Ndiko kulondola.”—Mkonzi.] Ameneyo ndi mwamuna wanu. Iye anali ndi chotupa, si choncho iye? Inde. Inu nonse mwachiritsidwa. Inu mukhoza kupita kwanu tsopano. Mulungu akhale ndi inu ndipo akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, mlongo.

Chikhulupiriro chophekwa chamukhudza ndi kumuchiza mkaziyu.

218 Bwerani. Inu muli bwanji, mlongo? Mwina ndife alendo kwa wina ndi mzake. Ife sitikudziwana wina ndi mzake. Tsopano, ine ndangokhala m’bale wanu. Ndi za mwana wanu, ndi zomwe inu mwadzera pano. Mdima wakuda wapachikika pa mwanayo. Ndi matenda osachiritsika, monga momwe madokotala akudziwira. Kodi inu mukukhulupirira Iye angaululire kwa ine chomwe chiri cholakwika ndi mwanayo? [Mlongo ati, “Inde.”—Mkonzi.] Ndi mtima wanu wonse, inu mukukhulupirira izi? [“Inde, bwana.”] Pakhala pali mtundu wina wa chochitika cha ku chipatala. [“Inde.”] Mwanayo anali ndi opareshoni. [“Inde, bwana.”] Ndipo ndi chinachake mmatumbo. Ndipo pali mtundu wina wa fupa kapena chinachake umo chomwe chikuvuta. Ndipo mwanayo ali ndi chiwindi chotupa tsopano. [“Inde.”] Si zoona izo? [“Inde, bwana.”] Icho nchoonadi, si choncho? [“Inde, bwana.”]

219 Tsopano, uyo si ine yemwe ananena izo. Uko kunali kungodzipereka kwathunthu kwa Yesu Khristu. Ndipo Kukhalapo Kwake kuli pano. Tsopano chinthu chokha chimene ine ndingakhoze kuchita ndi kumupempha Mulungu chifukwa cha mwana wanuyo. Inu mukulandira machiritso a mwanayo? [Mlongo ati, “Inde, bwana.”—Mkonzi.]

220 Khristu, Mwana wa Mulungu, muchitire chifundo pa mwana akufa uyu. Mulole iye akhale bwino usiku womwe uno. Perekani, Ambuye Yesu, kuti madalitso Anu abwere pa iye ndipo iye akhala bwino, pakuti ine ndikupempha izi mu Dzina la Yesu Khristu. Amen.

221 Mulungu akudalitseni inu, mayi. Mundirole ine ndidzamve za mwanayo, zomwe—zomwe zitachitike. Inu mukapeza kusiyana mmenemo, mu maora twente-foro otsatira. Tsopano kumbukirani zomwe ine ndakuuzani inu. Iye Yemwe akudziwa chomwe chinali, akudziwa chomwe chiti chikakhale. Chabwino.

222 Bwerani, dona. Inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Inu mukukhulupirira kuti Ambuye Yesu Khristu ali pano kuti akuchizeni ndi kukupangani wabwino? Inu mukundikhulupirira ine ngati wantchito Wake? [Mlongo ati, “Ine ndiri.”—Mkonzi.] Inu mukuzindikira kuti muli mu Kukhalapo kwa Chinachake kupatula munthu, ndipo uwo ndiwo Mzimu Wake.

223 Omvetsera mwina sangamvetse izi. Koma penyani maonekedwe pa nkhope ya odwalawo pamene iwo akuyenda pafupi ndi pano. Osati chifukwa ndi ineyo; ine ndiribe kanthu kochita ndi izo. Ine ndangokhala liwu. Koma mkazi uyu pano, kapena aliyense wa iwo, akumvetsa ndipo akudziwa kuti pali chinachake chazimu pano. Ndipo inu mukhoza kuziwona izo ngati chozizwitsa. Kodi chozizwitsa ndi chiani? Chinachake chomwe sichimamvetsedwa.

224 Tsopano, mkazi, mlendo kwa ine, ndi ine kwa mkaziyu; sitikudziwana wina ndi mzake; nthawi yoyamba mu moyo kuti tikomane, mwinamwake. Koma Mulungu watidyetsa ife tonse kuyambira pamene ife tinabadwa.

225 Dona, kodi inu mukukhulupirira kuti, Ambuye Yesu yemweyo yemwe anayankhula kwa mkazi pa chitsime, yemwe ine ndamuimira pano usikuuno, kuti firii handired. . . kapena miyoyo handiredi ndi firii inamulandira Iye monga Mpulumutsi? Kodi inu mukukhulupirira tsopano kuti Iye akuudziwa mtima wanu, ndipo akudziwa chirichonse chomwe inu mwachichita? Ngati Iye ati awululire kwa ine chimene inu muli kuchikhumba tsopano, kodi inu muzimomereza izo? [Mlongo ati, “Ine nditero.”—Mkonzi] Misempha. [“Ndiko kulondola.”] Ndi kulondola uko? [“Ndi kulondola.”] Inu mukundikhulupirira ine tsopano? [“Ndithu mukutero.”] Tsopano pano pali chinachakenso. Inu mukukondweretsedwa ndi wokonedwa wina, yemwe ali mnyamata. [“Ndiko kulondola.”] Ndipo mnyamata uyo ali ndi vuto la mtima. [“Ndiko kulondola.”] Ndipo iye ndi membala wa mpingo muno mu Louisville. [“Ndiko kulondola.”] Mpingo wa Baptisti. Pitani. Ambuye Yesu akudalitseni inu ndipo apereke kwa inu chokhumba cha mtima wanu. Amenii.

226 [M'bale pa nsanja ati, “Nenani, ‘Ambuye alemekezeke!’” Osonkhana ati, “Ambuye alemekezeke!”—Mkonzi.]

Ingokhalani molemekeza; landirani, khulupirirani.

227 Tsopano ine ndikumuwona dona, dona wachikuda, wakhala, akupemphera. Iye ali ndi vuto la impsyo. Inu mulibe ilo tsopano,

dona. Chikhulupiro chanu chakupangitsani inu kuchira. Imirirani. Mulungu akudalitseni inu. Ingokhulupirirani, ndi mtima wanu wonse, ndipo inu mukhala nazo izo.

Mzimu Woyera, chipembedzo cha Chipangano Chatsopano! Amen.

²²⁸ Inu mukukhulupirira kuti kuthamanga kwa magari uko kukuchokerani inu, bwana; mwakhala apo, mukuyang'ana pa ine? Inde. Chabwino, inu mukhoza kukhala nazo izo. Mulungu akudalitseni inu.

Ingomukhulupirirani Iye.

²²⁹ Khalani ndi chikhulupiro, mlongo, mwakhala apo mukuyang'ana mbali ino, mukupemphera, inunso. Muli ndi chinachake chavuta ndi mmero wanu, si choncho inu? Mwakhala kumbuyo komwe kwa msungwana wamng'ono uyo apo. Inu mukukhulupirira kuti Mulungu akupangitsani inu kuchira, dona wamng'ono wakhala apoyo? Inu mwakhala pamene mukupemphera kuti ine ndinene chinachake kwa inu. Ine ndikudziwa kuti ndi chikhalidwe cha mmero wanu. Inu simukusowa khadi la pemphero ayi. Inu mukungosowa chimene inu muli nacho, chikhulupiro. Kodi inu mukuvomereza machiritso anu tsopano? Mulungu akudalitseni inu. Inu mupite kwanu ndipo muchiritsidwe tsopano. Amen.

²³⁰ Khalani ndi chikhulupiro! Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse; Yesu Khristu apangitsa izo kuchitika. O, ine ndimamukonda Iye, si choncho inu? [Osonkhana ati, "Ameni."—Mkonzi.] Chabwino.

Bwerani, bambo.

²³¹ Khalani ndi chikhulupiro mwa Mulungu. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Mulungu apangitsa izo kuchitika.

²³² Inu muli bwanji, bwana. Kodi inu munali mmodzi wa oyima, maminiti angapo apitawo? Ine ndikuwona kukadalipo Kuwala pozungulira inu. Inu munamuvomereza Khristu ngati Mpulumutsi wanu. Inu mukuvutika ndi chikhalidwe cha manjenje. Si kulondola uko? Inu munali ndi chizolowezi choipa, chosuta. Mulungu sakufuna inu kuti muzichita izo. Izo zikuvulaza misempha yanu, kukupangitsani inu kumachita izo. Kodi si zoona izo? [M'bale ati, "Inde, bwana."—Mkonzi.] Inu mukufuna kuti muthane nazo izo; inu mukusiya ndudu, inu mukusiya chirichonse. Yesu Khristu wakhudza kale thupi lanu, ndipo inu mukakhala bwino ndipo muzikamtumikira Iye. Inu mukukhulupirira tsopano?

²³³ Kutu inu mukhoze kudziwa izi. Inu si ochokera mu mzinda uno. Ndinu ochokera kunja kwa tauni, si choncho inu? [M'bale ati, "Ndiko kulondola."—Mkonzi.] Ndinu ochokera ku Indiana. Inu munawoloka mtsinje. Ndinu ochokera ku mzinda wotchedwa Greensburg, kapena chinachake chonga izo, Indiana.

Ndi kulondola uko? Tsopano inu muli bwino. Eya. Tsopano inu mukhoza kupita kwanu ndi kukakhala bwino. Mulungu akudalitseni inu.

²³⁴ Omvetsera mukhale molemekeza, mukhale mu pemphero, mukhale mukuyembekezera Mulungu kuti akudalitseni ndi kukuchiritsani. Ameni. Khalani ndi chikhulupiro mwa Mulungu!

²³⁵ Inu mwakhala apo, dona, muli ndi chala chanu mmwamba monga *chonchi*, mukuvutika ndi. . . Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akuchiritsani inu kupopa magazi kotsika uko komwe inu muli nako? Kodi inu mukukhulupirira izo? Inde. Inu mukukhulupirira kuti Iye watero? Imirirani pa mapazi anu ndiye ndipo muzilandire izo. Izo zikusiyani inu, ndipo inu mukhoza kupita kwanu ndi kukakhala muli bwino.

Inu mukuti, “Nchiani chinachititsa izo?”

²³⁶ Yesu Khristu yemweyo yemwe anatembenukira kwa mkazi ali ndi kuwukha kwa magazi, anati, “Chikhulupiro chako chakupulumutsa iwe.” Anati Iye amadziwa zinthu zonse, ndipo Iye amaziulula izo momwe Iye amafunira. Chabwino.

Mbweretseni wodwala wanu. Khalani nacho chikhulupiro.

²³⁷ Inu muli bwanji, bwana? Kodi inu mukundikhulupirira ine kuti ndine wantchito Wake? [M'bale ati, “Inde, ine ndikutero, bwana.”—Mkonzi.] Inu mukukhulupirira kuti muli mu Kukhalapo Kwake, osati m'bale wanu. Koma inu mukuzindikira kuti chinachake chikuchitika? [“Inde, bwana.”]

²³⁸ Winawake amati ine ndinali ndikuwerenga maganizo anu pomwe pano. Uko ndiko kulakwitsa. Yesu Khristu “ankazindikira maganizo awo.” Nkulondola uko? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Anthu sali kuganiza za machimo awo ndi zinthu zomwe iwo anachita. Ndi Mzimu Woyera. Chabwino.

²³⁹ Tayang'anani mbali ino, bwana, ndipo mukhulupirire. Kodi ndife alendo kwa wina ndi mzake? [M'bale ati, “Inde, bwana.”—Mkonzi.] Ife sitikudziwana wina ndi mzake. Mwinamwake sitinayambe tawonanapo mu moyo wathu wonse. [“Msonkhano uno basi.”] Msonkhano uno wokha. [“Uko nkulondola, bwana.”] Ndiye ngati pali chirichonse chokhudza inu kapena chirichonse, matenda anu kapena chirichonse, Mulungu yekha angadziwe. Monga momwe ine ndikudziwira, ine sindikudziwa.

²⁴⁰ Koma ine ndikukuwonani inu mukutengedwera ku chipatala. Inu mwangotuluka kumene ku chipatala. [M'bale ati, “Uko nkulondola.”—Mkonzi.] Pali chinachake cholakwika ndi magazi, timakhunguto tikusweka, kapena chinachake. [“Uko nkulondola. Uyo ndi Ambuye.”] Ndipo inu munali. . . ine ndikukuwonani inu pa kama, ndipo apo pali mtundu wina wa chinachake chitapachikika pa inu, ndi chinachake woukha. . .

Ndi magari. [“Uko nkulondola.”] Ine ndikukuwona kuthiridwa magari wani, thuu, firii, foro, faifi, sikisi, seveni kumene inu mwakhala nako. [“Ambuye alemekezeke. Uko nkulondola. Uko nkulondola.”] Ndi zooni izo? [“Uko nkulondola. Amenewo ndi Ambuye.”] Ndi choonadi. [“Ndi zooni.”]

²⁴¹ Inu muli ndi mkazi yemwe akudwala. [M’bale ati, “Inde. Uko nkulondola.”—Mkonzi.] Iye ali ndi nyamakazi, ndi vuto la chiwindi. [“Kulondola.”] Ndi kulondola uko? [“Ndi kulondola.”] Ndipo sindinu ochokera mu mzinda uno. [“Ayi.”] Inu mwachokera kuntunda kwa mtsinje. [“Ndiko kulondola.”] Mwachokera ku Cincinnati. [“Ndiko kulondola.”] Ohio. [“Inde. Ndi Ambuye.”] Dzina lanu ndi Berghaus. [“Ndiko kulondola.”] R. P. ndi zoimira maina anu. [“Ndiko kulondola.”] Bwererani kwanu ndipo mukachiritsidwe [“Ndi Ambuye Mulungu.”] Yesu Khristu wakupangitsani inu kuchira.

²⁴² Mukhale ndi chikhulupiriro mwa Mulungu! Kumuuza iye dzina lake? Kodi Yesu sanamuze Petro, “Iwe ndiwe Petro”?

²⁴³ Tsopano khalani molemekeza, abwenzi. Masomphenya amakufooketsa iwe kwambiri. Inu mwakhlapo mu misonkhano, sabata ino, ndipo inu mukudziwa chimene ine ndikuchikamba. Mungokhala nacho chikhulupiriro mwa Mulungu! Khulupirirani! Ndipo apo panali chinachake... Mphindi chabe.

²⁴⁴ Ine ndikumuwona dona patsogolo panga. Ayi, ndi—ndi dona uyu wakhala apa pomwe pa mapetowa. Ndinu... Si inuyo; ndi munthu wowoneka mosiyana. Ndi wokonedwa wanu yemwe ali mu chipatala, ndipo iwo ali ndi khansara. Ndipo ndi dona, ndipo iye ali mu chikhulupiriro chakufa. Ndipo iye ndi mulamu wanu wamkazi. Ndi kulondola uko? Ngati izo ziri, imirirani pa mapazi anu tsopano ndipo mulandire machiritso a kwa mulamu wanu wamkazi mu chipatala. Ambuye Yesu Khristu Yemwe akudziwa zonse za izo!

²⁴⁵ [Mlango akusangalala—Mkonzi.] Chabwino, mlango, inu mukuwomba manja anu, mukusangalala. Inu munali ndi chinachake chovuta ndi manja anu, si choncho inu? Chabwino, iwo achiritsidwa tsopano, ndipo inu mukhoza kupita kwanu.

²⁴⁶ Ndipo inu amene mwakhala pafupi ndi iwo apo, inu munali ndi miyala mu kapamba. Si choncho inu, dona, mwakhala apo? Imirirani pa mapazi anu. Inu mukhoza kumapita kwanu, inunso, ndipo mukachiritsidwa. Izo zikusiyani inu, mu Dzina la Ambuye Yesu Khristu.

²⁴⁷ Ingokhulupirirani! “Zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo omwe akhulupirira.” Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu!

²⁴⁸ Mbweretseni donayo. Inu mukukhulupirira, dona, pamene inu mukubwera? Inu mukumuvomereza Yesu monga Mpulumutsi, ndipo mukundivomereza ine ngati mneneri Wake?

249 Ndiye ngati izo ziri chomwecho ndipo ine ndachitira umboni wa chiukitsiro cha Yesu Khristu; Iye Yemwe anaima ndipo anayankhula kwa mkazi pa chitsime, anadziwa ndendende chomwe chinali cholakwika ndi iye. Iye anati, “Pita ukamutenge mwamuna wako.” Iye anati, “Bwerani, mudzamuwone Munthu yemwe wandiuza ine chirichonse chimene ine ndachichitapo.” Iye sanamuuze konse iye zonse zomwe anazichitapo. Koma Iye ankadziwa, kuti Atate akanaululira kwa Iye, zonse zomwe iye anazichitapo. Kodi Iye ali Ambuye Yesu woukitsidwa yemweyo?

250 Inu munali ndi ngozi. Ayi, inu muli ndi chinachake chonga. . . Inu mwakhala muli. . . Ndi Mzimu Woyera ndi umene inu mukuufuna, ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndiko kulondola. Ndipo inu muli ndi. . . Ine ndinawona chinachake, inu muli—inu muli ndi kuthamanga kwa magazi, inunso, sichoncho izo?

251 Mphindi chabe, masomphenya anawonekera patsogolo panga. O, ndi mkazi wakhala apoyo, akupemphera. Ndi inuyo yemwe munali. . . Inu munapwetekedwa phazi lanu, sichoncho inu? Ngozi, ndipo mwapwetekedwa phazi lanu. Ndi kulondola uko? [Mlongo ati, “Ndiko kulondola.”—Mkonzi.] Ndipo inu muli ndi vuto la impsyo. Ndi kulondola uko? [“Inde.”] Chinabwera modutsa, ndi donayo, inu nonse mukupita kukachiritsidwa. Yesu Khristu. . .

252 Aleluya! O, ulemerero, Ambuye Yesu Khristu wosafanizitsidwa Yemwe anapulumutsa moyo wanu, kanthawi kapitako, akutsimikizira Kukhalapo Kwake. Amen. Mufufuze pa kujambula kwa tepi yanu ndipo muwone ngati zomwe Iye akunena si zoon. O, khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu! Khulupirirani! “Zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira.”

Chabwino, Billy, kodi uyu ndi wodwala wako? M’bweretse iye.

253 Mukukhulupirira, ndi mtima wanu wonse? Muli naye wokonededwa ali mu vuto, nayenso, si choncho inu? Iwo sali kuno mu mzinda, ngakhalenso. Ali ndi mtundu wina wa kunjenjemera. Ndi Manjenje, ngati. Ndi kulondola uko? Ndipo iwo amakhala mu mzinda komwe kuli mtsinje. Ndi mzinda waukulu, ndipo uko kuli mtsinje umapita mmphete mwa iwo. Ndipo kuli zochuluka za-. . . Ndi St. Louis. Ndi kulondola uko? Uko nkulondola.

254 Ndipo inu muli ndi wachibale wina, yemwe ali mlongo kapena chinachake, ndipo iye ndi wochokera ku dziko lomwe liri ndi mapiri mwa ilo, mitengo yobiriwira nthawizina. Ndi ku Arkansas. [M’bale ati, “Ndiko kulondola.”—Mkonzi.] Ndipo ali ndi vuto la mtima. [“Ndiko kulondola.”] Pitani, zokhumba zanu zaperekedwa kwa inu ndi Yesu Khristu Mwana wa Mulungu.

255 Tiyeni tinene, “Matamando akhale kwa Ambuye Yesu Khristu, Woukitsidwayo, Iye wochokera ku Kalvareyo!” [Osonkhana atamanda Ambuye Yesu—Mkonzi.]

256 Khalani molemekeza. Musati mutaketake. Miniti yokha, ndipo ife titseka mu maminiti pang’ono. Musati mutaketake monga choncho. Izo zimandisokoneza ine. Ine ndiri...pano usikuuno, ndikupenya. Khalani molemekeza.

257 Muloleni donayo abwere. Kodi inu mukukhulupirira kuti inu mukhoza kuchiritsidwa, ndi chikhulupiriro, ndipo chotupa icho chingakuchokereni inu popanda kung’ambidwa? Inu mukukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse? Inu mukuvomereza izo tsopano? Mu Dzina la Yesu Khristu, mulole izo zikhale kwa inu monga momwe chikhulupiriro chanu chanenera. Amenii.

258 Bwana, mwakhala apo, mwavala tayi yofiira; inu mukuvutika ndi—chotupa. Inu mukukhulupirira kuti Ambuye Yesu akupangitsani inu kuchira? Inu mukuvomereza izo? Ndinu ochokera kunjira kwa mzinda, inunso. Ine ndikuona inu mukuchokera kuntunda kwa mtsinjewu, inunso, Cincinnati. Si kulondola uko? Chabwino. Pamene inu mukugwira ntchito awiri, nonsenu imirirani pa mapazi anu pakali pano ndipo muchiritsidwe mu Dzina la Yesu Khristu. Mulungu akudalitseni inu. Izo zikukuchokerani inu. Pitani kwanu; mukachiritsidwe.

259 Bwerani, dona, muli ndi chikhulupiriro. Inu mukukhulupirira kuti vuto lachikazi ilo lakusiyani inu? Inu mukuvomereza Yesu ngati mchiritsi wanu kwa izo tsopano? Icho chinali chotokusira, chinali ndi powukhira, ndipo izo zikanatsirizira kukhala khansara posachedwapa. Koma chikhulupiriro chanu chakupulumutsani inu. Tsopano pitani, zikampatsani Mulungu matamando pa izo, ndipo inu mukakhala nazo zirizonse zomwe inu mukuzipempha.

260 Bwerani, bwana, mukukhulupirira ndi moyo wanu wonse. Ngati Mulungu ati aulule lomwe liri vuto lanu, kodi inu mulandira machiritso anu? Vuto la mtima. Ndi kulondola uko? Inu mukukhulupirira Iye akuchizani inu tsopano? Ndiye, Iye watero. Chikhulupiriro chanu chakupangitsani inu kuchira. Pitani, mukakhale mu mtendere wa Mulungu.

261 Bwerani, dona. Inu mukukhulupirira Mulungu amuchiritsa mwana uyo pamene ine ndikubwera kudutsa pa nsanja? Iye ali ndi vuto la impsyo. Pitani tsopano, Yesu Khristu alichiritsa khanda laling’onolo, mu Dzina la Yesu Khristu. Amenii. Inu munali wamanjenje; izo zakusiyani inu, aponso. Mulungu akhale ndi inu.

262 Inu mukumukhulupirira Iye? [Osonkhana ati, “Amenii.”—Mkonzi.] Khalani ndi chikhulupiriro mwa Mulungu!

263 Inu mukufuna kuti muthane nalo vuto la mapapo ilo? Inu mukukhulupirira Mulungu akukuchizani inu kwa izo? Ngati inu

mukukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse, imani pa mapazi anu, dona. Landirani machiritso anu. Mulungu akudalitseni inu. Inu mukhoza kupita kwanu tsopano ndi kukachiritsidwa. Chabwino. Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse? Kodi inu mukuvomereza machiritso anu ngati Yesu Khristu, akuyankhula, ati aulule vuto lanu? Ndife alendo kwa wina ndi mzake, koma, Iye akulidziwa vuto lanu. Inu muli ndi vuto lachidona, lachikazi, chiberekero ndi thumbo. Tsopano, pitani, Mulungu wakupangitsani inu kuchira. Chikhulupiriro chanu chakupulumutsani inu, dona, mu Dzina la Yesu Khristu.

²⁶⁴ Tiyeni tinene, “Ambuye alemekezeke!” [Osonkhana ati, “Ambuye alemekezeke!”] Wina aliyense wa inu akhoza kuchiritsidwa pa nthawi ino, ngati inu muti mukhulupirire.


²⁶⁵ Tsopano, dona, imani pomwe inu mulipo, yang’anani mbali ino. Omvetsera onse awa, gawo lalikulu la iwo, likuvutika ndi manjenje awo. Nthawizina inu mumaganiza kuti malingaliro anu asokonezeka, sichoncho inu? Inu mumakhala wamanjenje kwambiri. Posachedwapa inu munagwetsa chinachake; iyo inali mbale kapena chinachake, inu mumayenda nayo iyo. Koma tsopano Yesu Khristu wakuchiritsani inu kwa izo, ndipo inu mukudziwa izo. Tsopano pitirirani pa ulendo wanu, mukusangalala.

²⁶⁶ Tsopano, mu Dzina la Yesu Mwana wa Mulungu, ine ndikumutsutsa wokhulupirira aliyense muno kuti akhulupirire kuti izi ndi Choonadi. Kodi inu mukuzikhulupirira izo? [Osonkhana ati, “Ameni.”—Mkonzi.] Chabwino, ndiye, ngati ichi chiri Choonadi chotsimikiziridwa ndi Mulungu, ndimvereni ine. Ikani manja pa wina ndi mzake, pamene ine ndikukupemphererani inu. Ndipo ine ndikufuna munthu aliyense muno tsopano kuti mulandire machiritso anu.

²⁶⁷ Mulungu Wamphamvuzonse, chitirani chifundo kwa odwala ndi osowa. Aima pano, ndipo chipinda chonse chino chikuwoneka kuti ndi Lawi la Kuwala limodzi lalikulu tsopano. Podziwa kuti winawake waima pafupi ndi manja awo pozungulira ine, nditatsamira pa mipango; idalitseni iyo, Ambuye, kwa kuchiritsidwa kwa odwala. Anthu onse osowa awa, ali ndi mikono yawo ndi manja itaikidwa pa wina ndi mzake. Mulole Mphamvu, njira yoperekedwa ndi Mulungu, Mwana wa Mulungu, mu Mphamvu Yake yaikulu ndi ufumu, zisese mchipinda chino ngati mphepo ya mkokomo wamphamvu, ndi—ndi kutsutsa nthenda iliyonse, kutulutsa mzimu woipa uliwonse.

²⁶⁸ Tsopano ine ndikumutsutsa Satana, ndikutenga chigonjetso pa iye pakali pano. Ndipo tuluka, Satana, mwa anthu awa, mu Dzina la Yesu Khristu.

²⁶⁹ Ndipo mulole wina aliyense muno, yemwe akukhulupirira kuti Yesu akuchiza iwo, aime pa mapazi awo ndi kumamupatsa Mulungu matamando, mu Dzina la Yesu Khristu.

²⁷⁰ Mulungu, mu Dzina la Yesu Khristu, iwo tsopano akuvomereza machiritso awo. 

MULUNGU ALINAYO NJIRA YOPEREKEDWERATU CHA54-0404E
(God Has A Provided Way)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham unaperekedwa mu Chingerezi Lamlungu usiku, Epulo 4, 1954, ku Memorial Auditorium mu Louisville, Kentucky, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©2014 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org